



CHAKA CHA SANDE SUKULU



MALANGIZO OPHUNZITSIRA

SANDE SUKULU

MALANGIZO OPHUNZITSIRA

SANDE SUKULU

ZA M'KATIMU

PHUNZIRO	TSAMBA
1. CHAKA CHA SANDE SUKULU.....	7
2. KUPHUNZITSA SANDE SUKULU ANA AMENE ASANAYAMBE SUKULU.....	11
3. KUPHUNZITSA ANA SANDE SUKULU.....	25
4. KUPHUNZITSA ACHINYAMATA SANDE SUKULU.....	41
5. ZOPHUNZITSIRA APHUNZITSI A SANDE SUKULU YA AKULU.....	57
6. KUCHITIRA UMBONI KWA ANTHU AMENE SANALANDIRE YESU KHRISTU KUPYOLERA M'SANDE SUKULU (WOLEMBA NDI BAMBO ROSS COLLIER).....	74

CHAKA CHA SANDE SUKULU

CHAKA CHA SANDE SUKULU

KODI CHOLINGA CHAKE NDI CHIYANI?

1. Tili kufuna kuyambitsa Sande Sukulu kuyambira ya ana mpaka ya akulu m'tchalitchi iliyonse.
2. Tili kufuna kufalitsa Uthenga Wabwino kwa anthu onse.
3. Tili kufuna kuti tithandize matchalitchi athu kuti akule. Tili ndi chikhulupiriro kuti tikhoza kukulitsa matchalitchi athu kupyolera m'Masande Sukulu.

KODI CHOLINGA CHA SANDE SUKULU NDI CHIYANI?

1. Cholinga cha Sande Sukulu ndi "kusonkhanitsa" anthu athu kuti adzigwilira ntchito pamodzi. "Kusonkhanitsa" kumatanthauza kuti kukhazikitsa anthu a mpingo pamodzi kuti agwilire ntchito pamodzi.
2. Ntchito imene tili kufuna kuti agwireyo ndi yakuchitira umboni wa Yesu Khristu kwa anthu awo. Imeneyi ndi ntchito yofunika kwambiri m'tchalitchi. Tiyenera kusonkhanitsa anthu athu pamodzi, kuti tiwaphunzitse, ndi kuwatumizanso kwina kuti akachitire umboni anthu enanso. Kuwasonkhanitsa pamodzi! Ichi ndiye cholinga chake cha Sande Sukulu.

SANDE SUKULU NDI YA ANTHU ONSE

Chotsani maganizo akuti Sande Sukulu ndi ya ana okha. Akuluakulu nawonso ayenera kumaphunziranso Sande Sukulu. Sande Sukulu ndi ya munthu aliyense.

1. Anthu okalamba, achinyamata, akuluakulu, ndi ana.
--- Banja lonse --- anthu onse.
--- Mamembala a mpingo --- anthu osapulumsidwa.
2. Amagawidwa m'magulu ang'onoang'ono amene amatchedwa kuti makalasi. Kalasi iliyonse ili ndi ntchito imene imagwira.

KODI NTCHITO YA SANDE SUKULU NDI CHIYANI?

1. Kuphunzitsa anthu kuwerenga Buku Lopatulika m'magulu kapena pa okha.
2. Kuwaphunzitsa Buku Lopatulika. Buku Lopatulika ndilo Buku limene liyenera kuwerengedwa pa Sande Sukulu.

4. Muwaphunzitse ndi kuwalimbikitsa monga chiwalo chimodzi cha mpingo. Munthu akalandira Yesu Khristu monga Mpulumutsi wake sindiye kuti inu ntchito yanu yathera pompo ayi. Tili kufuna kuti akhale chiwalo cha mpingo, abatizidwe ndi kuyamba kutumikira Ambuye.
5. Muyenera kuwatumikira. Kuwathandiza, kuwatumikira, kuwathandiza pa zosowa zawo, ndi kuwaphunzitsa kutanthauza kwake kwa kukhala otsatira wake wa Yesu Khristu.

SANDE SUKULU NDI YOFUNIKA KWAMBIRI

- (1). Tchalitchi yanu ifunika kuti ikhale ndi Sande Sukulu. Chaka chino chimene chili chaka cha Sande Sukulu tili kufuna kuti tikuthandizeni kuti muyambe Sande Sukulu. Tili kufuna kuti tikuthandizeni kuphunzitsa anthu anu kuti akhale aphunzitsi, kuchezera anthu, kuchitira umboni ndi kukulitsa tchalitchi.

KUPHUNZITSA SANDE SUKULU ANA
AMENE ASANAYAMBE SUKULU

KUPHUNZITSA SANDE SUKULU ANA AMENEASANAYAMBE SUKULU

1. ZIMENE BUKU LOPATULIKA LIMANENA CHIFUKWA CHAKE

CHOPHUNZITSIRA ANA ANG'ONO

- (1). Yesu anatisiira chitsanzo kuti tidziwe kuti ana ndi ofunika kwambiri
- (2). M'Chipangano Chakale muli malamulo ochokera kwa Mulungu za udindo ophunzitsa ana Buku Lopatulika.
- (3). Ana ang'ono amatha kuphunzira Buku Lopatulika ndi zoonadi zake.

2. ZOYENERA KUCHITIKA PA SANDE SUKULU

- (1). Kupeza ana ang'ono amene asanayambe kupita ku sukulu.
- (2). Kuwaphunzitsa Buku Lopatulika.
- (3). Kuwaphunzitsa kuti adziwe kuti Mulungu amawakonda ndipo amasamalira mwana aliyense.
- (4). Kuwaphunzitsa kuti adziwe kuti kutchalitchi ndiye malo opembedzerako Mulungu, ndipo ndi malo amene munthu akhoza kupezako chimwemwe.
- (5). Kuwachitira umboni ana pamodzi ndi mabanja awo.

3. ZOYENERA MPHUNZITSI

Mphunzitsi wabwino ndi amene ali ndi:

- (1). Ndi mkhristu amene analandira Ambuye kukhala monga Mpulumutsi wake ndi Mfumu ya moyo wake ndipo ndi chiwalo cha mpingo wa Baptist.
- (2). Amakonda ana.
- (3). Ndi munthu amene amakonzekera kuphunzitsa Sande Sukulu sabata ndi sabata.
- (4). Ndi munthu amene amabwera ku tchalitchi mokhulupirika, kumapemphera pa sabata komanso mapemphero apakati pa sabata ndi kumaphunziro a Buku Lopatulika.

4. MAKHALIDWE A MWANA WAMNG'ONO (ENA AMATI AKACHISI)

Ana a kalasi imeneyi ayenera kukhala ndi zaka zoyambira pa 4-6.

- (1). Pa zaka zimenezi mwana satha kukhala pamodzi; sangathe kukhala pamodzi nthawi yaitali.
- (2). Muyenera kulankhula mofatsa ndiponso chichewa chake chikhale chapafupi, mukhoza kumalankhula monga m'mene amalankhulira kunyumba kwawo.
- (3). Pa zaka zimenezi ana amakhala odzikhulupirira; amaganizira za iwo okha. Nthawi zambiri akamalankhula amakonda kuti 'ine' kapena kuti ndi "changa."
- (4). Ana amachita zinthu mofulumira. Amafuna kuti achite zinthu zimene zingakondweretse mphunzitsi.

5. MAKONZEDWE AKE

- (1). Zaka zawo ndi kukula kwake kwa kalasiyo.
- (2). Malo okumanilako.
- (3). Nthawi.
- (4). Zofunikira zake za pa Sande Sukulu,
 - (a). Buku Lopatulika.
 - (b). Buku la Sande Sukulu la mphunzitsi.
 - (c). Buku lolemberamo maina.
- (5). Kuwakweza ana aja kuti adzipita ku makalasi ena apamwamba (polomoshoni).

6. MAGAWO A MAPHUNZIRO

Pali magawo amaphunziro amene anthu ayenera kuphunzira paphunziro lililonse. Phunziro lililonse limakhala ndi magawo anai kapena asanu.

7. KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

- (1). Muyenera kuwerenga bwinobwino Buku Lopatulika ndi buku la Sande Sukulu.
- (2). Muwerenge ndime zonse za m'Buku Lopatulika zimene zili m'buku muja.
- (3). Muyenera kuona cholinga cha phunziro lija.
- (4). Mudzilemba zinthu zimene mukaphunzitse ndi kukonzekera bwino sabata ndi sabata.

- (5). Mukonzekere masewero osiyanasiyana amene angathe kuthandiza ana kuti aphunzire bwino.
- (6). Mukhale ndi nthawi yoyambira Sande Sukulu ija ndipo muyenera kuitsata nthawiyo.
- (7). Muyenera kukonzekera kumafika ku Sande Sukulu mofulumira sabata iliyonse.

8. NTHAWI YAKE

Nthawi yophunzitsa iyenera kukhala pakati pa 40-60 minisi.

- (1). Mufike mofulumira ndipo mukonze bwino pa malo ophunzilirapo paja.
- (2). Muyenera kugwiritsa ntchito zinthu kapena kuchita sewero pa kuphunzitsa.
 - (a). Nthano.
 - (b). Sewero.
 - (c). Kuyimba nyimbo.
 - (d). Kuthamanga ndi zina zotere.
 - (e). Zojambulajambula.

9. KUCHEZERA ALENDU

Mphunzitsi aliyense ayenera kukachezera mwana kapena munthu aliyense amene ali pa Sande Sukuluyo kunyumba kwawo. Ichi chidzamupatsa mwayi wakuchitira umboni banja lonse.

KALASI 1.

Ana amene asanayambe sukulu (akachisi).

KALASI 2.

Ana akulupo amene amapita ku sukulu.

KALASI 3.

Achinyamata

KALASI 4.

Akuluakulu amayi ndi abambo.

Inuyo mwasankhidwa kuti mukaphunzitse aphunzitsi amene adzikaphunzitsa ana ang'ono amene angoyamba Sande Sukulu; (akachisi) amene ali ndi zaka kuchokera 4-6. Ana ang'ono kupambana apa sayenera kuti akhale pa kalasi imeneyi.

Mudzalandiranso pepala lina limene lili ndi zinthu zonse zimene anafotokozera bwino za zimenezi. Muyeneranso kuwerenga buku la Sande Sukulu limene limatsogolera

aphunzitsi pakuphunzitsa, ndi buku linanso la ana amene asanayambe sukulu.

Ndikofunika kwambiri kuphunzitsa ana. Mwana amaphunzira kwambiri ndiponso amamvetsetsa msanga pamene ali wamng'ono makamaka pamene ali ndi zaka 4-6. Taganizira-ni za mwana wamng'ono. Kodi amaphunzira bwanji kuyenda? Amaphunzitsidwa ndi makolo ake. Amaphunzira kulankhula pakumverera kwa anzake. Amaphunzira kuchita zinthu kuonelera kwa anzake.

Ana amene asanayambe sukulu akhoza kuphunzira zinthu za Uzimu. Amaphunzira zimenezi kuchokera kwa anzawo. Kuyambira zaka 4-6 ndi zaka zofunika kwambiri kuphunzitsa mwana kutsatira ziphunzitso za Mulungu.

1. NDIME ZA M'BUKU LOPATULIKA ZOYENERA KUPHUNZITSA ANA

- (1). Yesu anatisiyira chitsanzo. Anaonetsa ophunzira ake kuti ana ndi ofunika kwambiri. Werengani Marko 10:13-16. Yesu anadzudzula ophunzira chifukwa chakuti anapirikitsa ana. Pa ndime 14 anati, "Lolani tiana tidze kwa Ine; musatiletse. Pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa totere."
- (2). M'Chipangano Chakale Mulungu anapereka malangizo apadera akaphunzitsidwe ka ana. Miyambo 22:6, "Phunzitsani mwana poyamba njira yake, ndipo angakhale atakalamba sadzachokamo." Kuphunzitsa ana ndi udindo wa mpingo pamodzi ndi makolo. Deuteronomo 31:12-13. "Sonkhanitsani anthu, amuna ndi akazi ndi ana ang'ono ndi mlendo wokhala m'midzi mwanu, kuti amve, ndi kuti aphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu, ndi kusamalira kuchita mawu onse a chilamulo ichi; ndi kuti ana awo osadziwa amve, naphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu, masiku onse akukhala ndi moyo inu ku dziko kumene muonekera Yordano kulilandira likhale lanulanu."
- (3). Ana amene asanayambe sukulu amatha kuphunzira zinthu za Mulungu. Ayenera kuphunzitsidwa bwino kuti adzimvetsetsa msanga. Kuphunzitsa ana ndi madalitso apadera. Muli ndi mwayi wa kuphunzitsa ana m'njira za Mulungu.

2. NTCHITO YA SANDE SUKULU

Werengani mutu woyamba wa pa 6 za Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu. Pali zinthu zisanu zimene Sande Sukulu iyenera kuchita. Izi ndi zinthu zimene mphunzitsi wophunzitsa ana ayenera kuchita.

1. KUPHUNZITSA ANA BUKU LOPATULIKA

Monga mphunzitsi muyenera kuona kuti ana onse kuyambira a zaka 64-6 ayamba kuphunzira Sande Sukulu. Ngakhale makolo ake a mwanayo sabwera kutchalitchi koma mwanayo ayenera kulimbikitsidwa kuti adzibwera ku Sande Sukulu. Koma mukhoza kuwapempha makolo aja kuti abwere kutchalitchi kudzapemphera nawo. Mukhoza kupeza mwayi wakuwachitira umboni. Ana amene ali ndi zaka 4 ayenera kumabwera kutchalitchi ndi makolo awo.

2. KUWAPHUNZITSA KUWERENGA BUKU LOPATULIKA

Ana akhoza kuphunzira Buku Lopatulika. Ndi chinthu chofunika kwambiri kuphunzira. Muyenera kukumbukira zimenezi. Mwana akhoza kuphunzira zinthu zambiri kuposana ndi kungoyimba nyimbo chabe. Akhoza kuphunzira ndime za m'Buku Lopatulika ndi nkhani za m'Buku Lopatulika. Akhoza kumvetsetsa bwino Mawu a Mulungu pokhudzana ndi zinthu zimene amachita pa moyo wake. Mwachitsanzo, ana ambiri ali ndi mantha. Mwina amachita mantha ndi asing'anga, alendo, kapena njoka ndi agaru. Ndime imene akhoza kuiphunzira ndi iyi, "N'nthawi imene ndili kuchita mantha, ndidzakhulupirira Mulungu." Mwana akhoza kuphunzira ngati aphunzitsidwa m'njira yabwino.

3. KUWAPHUNZITSA KUTI MULUNGU AMAWAKONDA NDIPO
AMAWASAMALIRA

Mwana amadziwa ndipo amamvetsetsa m'mene makolo ake amamukondera. Amamupatsa chakudya kuti adye ndiponso malo ogona. Mwanjira yomweyi, akhoza kudziwa kuti Mulungu amamukonda. Imeneyi ndiyo nthawi yakubzyala mbewu. Akakula, adzadziwa kuipa kwake kwa tchimo ndi kufunika kwake kwa chipulumutso. Adzamanga maziko ake pa phunziro amene anaphunzira poyambapo nthawi imene anali mwana.

4. MUYENERA KUZINDIKIRA KUTI KUTCHALITCHI NDI MALO
WOPEMPHERERAKO

Ichi ndi chinthu chimene mwana akhoza kuphunzira pakuonera makolo ake ali kupita kutchalitchi. Tsono inu monga, mphunzitsi muyenera kuonetsa chitsanzo. Timalankhula za tchalitchi monga "nyumba ya Mulungu." Ichi chimatanthauza kuti tchalitchi ndi nyumba yapadera. Ana ayenera kukhala ndi nthawi yabwino. Ayenera kukhala okondwa pakubwera kutchalitchi.

5. KUCHITIRA UMBONI KWA MWANA WAMNG'ONO NDI BANJA LAKE

Iyi ndi ntchito yapadera ya mphunzitsi ndipo ndi gawo lofunika kwambiri. Mphunzitsi kuti achite zimenezi ayenera kumakawachezera ana aja kunyumba kwawo. Ngati mwana m'modzi sanabwere ku Sande Sukulu, potsiriza mphunzitsi ayenera kupita kunyumba kwawo kuti akamufunse chifukwa chake sanabwerere ku Sande Sukulu. Ana ang'onoang'ono amakhala ndi mabvuto awoawo. Mwina abambo amamwa mowa tsono akaledzera amamumenya mwana uja kapena amayi ake. Mwana uja akhoza kudwala ndi kulephera kubwera ku Sande Sukulu. Ngati mphunzitsi atapita kukacheza ndi makolo a mwana uja, akhoza kuwachitira umboni ndi kuwathandiza pa zinthu zina.

3. ZOYENERA MPHUNZITSI

Monga mphunzitsi wa ana ang'onoang'ono ndinu munthu wofunika kwambiri. Udindo wanu ndi waukulu kwambiri. Pali zinthu zomuyenereza kuti aphunzitse Sande Sukulu. Muwerenge mutu 7 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

- (1). Choyamba, pa zinthu zonsezi, mphunzitsi ayenera kukhala mkhristu amene anabadwanso kachiwiri. Ayenera kukhala chiwalo chimodzi cha mpingo wa Baptist.
- (2). Mphunzitsi ayenera kukhala munthu wokonda ana. Ayenera kukhala kuti ali kuphunzitsa ana ang'ono, osati achinyamata kapena akuluakulu. Ayenera kukhala munthu amene ali kumva maitanidwe akuphunzitsa ana.
- (3). Mphunzitsi wabwino amakonzekera phunziro lake sabata ndi sabata. Anthu ambiri amaganiza kuti Sande Sukulu ya ana ndi nthawi ya kuyimba nyimbo basi. Zimenezi sizooni. Mphunzitsi wa Sande Sukulu ya ana ayenera kuwerenga bwino Buku Lopatulika ndi kukonzekera phunziro lakelo bwinobwino. Mphunzitsi wa ana ayenera kukonzekera kwambiri chimodzimodzi ndi m'mene akadachitira ngati mphunzitsi amene ali kuphunzitsa kalasi ya akulu. Tsono muyenera kukonzekera sabata ndi sabata.
- (4). Ndi chinthu chofunika kwambiri kuti mphunzitsi ayenera kukhala wokhulupirika pakubwera ku Sande Sukulu. Ichi chitanthauza kuti mphunzitsi ayenera kumakhala pa kalasipo sabata iliyonse. Ngati mphunzitsi sanabwere ndiye kuti munthu wina amene sanakonzekere ayenera kuphunzitsa. Zotsatira zake ndiye kuti ana aja saphunzira.

Mphunzitsi wabwino amawerenga Buku Lopatulika lake ndi kupemphera tsiku ndi tsiku. Kumbukirani kuti kuphunzitsa Sande Sukulu ndi ntchito yabwino. Mphunzitsi ayenera kumathandizidwa ndi Mulungu.

4. MAKHALIDWE A MWANA WAMNG'ONO

Muyenera kukumbukira kuti Sande Sukulu imeneyi ndi yophatikiza ndi ana amene asanayambe sukulu. Pali magulu awiri a ana pamenepa. Pali ana amene ali ndi zaka 4-6 ndi ena amene ali ndi zaka zitatu mpaka kutsika m'munsi. Ngati tchalitchi yanu singathe kukhala ndi makalasi awiri, kalasi ya ana a zaka 4-6 ndi kalasi ya ana a zaka 3 mpaka kutsika m'munsi. Ana a zaka 3 ayenera kukhala ndi amayi awo. Ichi ndi chinthu chofunika kwambiri. Mpingo uyenera kuchita khama kuti uchite zimenezi. Matchalitchi ambiri akhoza kungokhala ndi kalasi imeneyi ya ana a zaka 4-6 (akachisi).

1. Ana amenewa amakhala a zaka 4-6. Ambiri mwa iwo amakhala atayamba kale kupita ku sukulu ya mkaka. Ndi ana amene amakhala achangu. Izi zimatanthauza kuti sangathe kukhala pamodzi nthawi yaitali. Amafuna kuti adzigwiragwira ndi kumachita zinthu. Akakhala chete, sangathe kuphunzira bwino. Nthawi zambiri ana akhoza kukhala chete chifukwa cha kufuna kulemekeza mphunzitsi, koma amamvetsera bwino pa mphindi 5-10 basi.
2. Pakuphunzitsa ana muyenera kumalankhula chichewa cha pafupi kuti adzimvetsetsa bwino. Ndi chinthu chofunika kwambiri mphunzitsi kumalankhula chilankhulo chimene ana aja amachidziwa. Kumalankhula mofatsa ndi modekha.
3. Pa nthawi imeneyi ana amakhala odzikhulupirira. Amakonda kunena kuti ndi "changa" kapena "ine." Ali kuyamba kuzindikira za anthu ena.
4. Mwana amafuna kuti akondweretse mphunzitsi wake. Amaphunzira pakuonera zimene ali kuchita aphunzitsi akewo.

5. CHIKONZEKERO

Werengani mutu 5 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

ZAKA; KUKULA KWAKE KWA KALASIYO: Gulu limeneli ndi la ana amene asanayambe Sande Sukulu. Ana ake ndi amene ali ndi zaka 4-6. Ana ang'ono kuposa pamenepa ayenera kusamalidwa ndi makolo awo.

Kalasi iliyonse iyenera kukhala ndi anaosapose 20. Ngati muli ndi ana ambiri muyenera kukhala ndi makalasinso ambiri. Mphunzitsi sangathe kuphunzitsa bwino ngati kalasi yake ili ndi ana ambiri. Tsono muyenera kukhala ndi aphunzitsi ambiri ndiponso muyenera kukhala ndi makalasi ambiri.

2. MALO OPHUNZIRIRAPO: Pakuti ana ake amakhala ogwiragwira, tsono muyenera kukhala ndi malo apadera ophunzirila. Izi ziyenera kukonzedwa ndi mkulu wa Sande Sukulu ndi abusa. Komabe inu monga mphunzitsi wa Sande Sukulu mukhoza kuwathandiza pakusankha malo amenewa. Malo ake ayenera kukhala akulu bwino kuti ana akhoza kumayenda ndi kusewera bwino. Ana ayenera kukhala pa malo abwino kuti akamayimba asasokosele anzawo. Anthu amakonda kuti Sande Sukulu ya ana idzikhala panja kapena m'zipinda za m'tchalitchi momwemo. Tchalitchi iliyonse ikhoza kusankha malo amene ali abwino. Ngati ndi panja mudziwayalira mphasa. Nthawi zambiri ana sangathe kukhala m'mipando chifukwa ndi yaitali. Mphunzitsi nayenso akhoza kumakhala nawo pa mphasapo. Ndi chinthu chofunika kwambiri kuti mphunzitsi adzikhala pamodzi ndi ana.
3. NTHAWI YOYAMBIRA: Mpingo uyenera kupangana nthawi yoyambira Sande Sukulu. Nthawi zambiri Sande Sukulu iyenera kuyambika mofulumira nthawi ya mapemphero isanayambe. Nthawi yophunzira Sande Sukulu iyenera kukhala mphindi 40-60. Maphunziro amene ali m'buku la aphunzitsi anakonzedwa kuti ayenera kuphunzitsa nthawi imeneyi. Tsono muyenera kutsatira zimenezi; kuyamba ndi kutsiriza nthawi yabwino.
4. Mphunzitsi aliyense ayenera kukhala ndi mabuku atatu. Mpingo uyenera kuwapatsa ngati kuli kotheka.
 - (a). Buku Lopatulika - Mphunzitsi aliyense ayenera kukhala ndi Buku Lopatulika, musayembekezere kuti mpingo ukupatseni lina. Mphunzitsi ayenera kuwerenga Buku Lopatulika tsiku ndi tsiku.
 - (b). Mabuku a mphunzitsi ndi mapepala ena. Pali mabuku amene aphunzitsi ayenera kutenga ochokera ku I.P.S. kapena ku Baptist Publishing House. Pali maphunziro 13 pa buku lililonse. Pali buku lina limene analemba kuti, "Kuphunzitsa ana amene amapita ku Sukulu ya mkaka, ana oyamba kumene." Ndi buku la aphunzitsi limene lifunika kugwiritsa ntchito zithunzi pa nthawi yakuphunzitsa. Linakonzedwera mipingo imene ili ndi malo ambiri kapena makalasi ambiri kumene kumafunika

aphunzitsi ambiri. Mpingo uli wonse uyenera kugwirizana za buku limene ali kufuna kuti agwiritse ntchito.

Tengani kabuku kamene akali ndi zithunzi mbali inayi ndi nkhani za m'Buku Lopatulika mbali inanso. Ndi chimodzimodzi ndi buku la aphunzitsi. Buku limeneli ndi labwino kwa aphunzitsi chifukwa likhoza kuwathandiza pa kubwereza zimene anaphunzitsa kale.

(c). Buku lolebamo maina. Kalasi iliyonse iyenera kukhala ndi buku lolebamo maina ndi kumaona m'mene ali kubwerera anthu. Chaka chili chonse muyenera kukhala ndi buku latsopano. (Ndi kwabwino kuyamba Sande Sukulu yanu pamodzi ndi masukulu a boma). Mulembe dzina la mwana aliyense mubuku limeneli. Sabata iliyonse mudzilemba maina a ana amene abwera ndi amene sanabwere. Pali mabuku enanso amene ali othandiza kwambiri. Mutenge mapepala kuti mupatse mwana aliyense akhale ndi pepala limodzi kuti lidzimuthandiza pakuphunzitsa. Ndi kwabwino kumapatsa mwana aliyense sabata ndi sabata kuti adzipita nawo kunyumba kwawo. Mukhoza kuwapezanso ku Baptist Publications. Muyeneranso kuwapatsa chithunzi chimene chili kugwirizana ndi phunziro la sabata imeneyo. Maphunziro amenewa amakhala m'magulu okwana 13 kufanana ndi maphunziro 13 amene mphunzitsi amakhala nawo pakuphunzitsa ana. Tsono ngati kuli kotheka mudzikhala ndi mapepala okwanira mwana aliyense kapena mabuku okwanira mwana aliyense.

(d). Kuphunzitsa pakugwiritse ntchito zithunzi - Izi ndi zithunzi zazikuluzikulu; Ndi chimodzimodzi ndi mapepala amene amatenga anthu kupita nawo kwawo. Muyenera kudziika pabwino. Mukhoza kudzigwiritse ntchito pa nthawi yaitali. Zithunzi ndi mapepala ndi zinthu zofunika kwambiri pakuphunzitsa. Nyuzi pepala ndi mapensulo kapena mkala zikhoza kugwiritsidwa ntchito pakunjambula zithunzi ndi zinthu zina.

5. MAGAWO OPHUNZIRA

Maphunziro ambiri amene ali m'buku la mphunzitsi amakhala pafupifupi phunziro limodzi. Zimenezi zimatchedwa kuti magawo. Pali magawo atatu pa buku lililonse la mphunzitsi. Ndi kofunika kuwerenga maphunziro onsewa ndi kuona chifukwa chake zimayendera limodzi. Mwachitsanzo, gawo limodzi likhoza kukhala lakuti, "Kuphunzira za chikonzero cha Mulungu pa mabanja." Nkhani zake ndi za Adamu ndi Hava, Davide

pamene anali wamng'ono, ndipo za Samueli pamene iyenso anali mwana. Muyenera kukonzekera masewero ndi zinthu zina kuti ana aphunzire za mabanja amenewa.

6. KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

Muli kuyamba kumvetsetsa kuti kuphunzitsa ana ndi ntchito yaikulu. Kutu mukhale mphunzitsi wabwino muyenera kumakonzekera tsiku ndi tsiku. Mphunzitsi ayenera kumayambira lolemba kukonzekera.

- (1). Poyamba, muyenera kuwerenga buku lanu bwinobwino pamodzi ndi Buku Lopatulika. Mudziwerenga liwu lililonse.
- (2). Tsono, muwerenge ndime zonse za m'Buku Lopatulika. Muwerenge Buku Lopatulika tsiku ndit tsiku. Muloweze pamtima ndime zonse zimene zili pa phunziropo.
- (3). Muwerenge cholinga cha phunzirolo. Muwerenge cholinga cha gawolo. Muyankhe funso ili, kodi ndiphunzitsa chiyani? Mulembe yankho lake.
- (4). Mulembenso phunziro lanu. Phunziro limenelo muyenera kulemba m'buku kapena m'kope. Muyankhe mafunso awa: Kodi ndiyamba bwanji? Kodi tikayimba nyimbo zotani? Kodi ndikanena nthano imeneyi nthawi yankho lake? Kodi tikachita masewero otani? Kodi nthano imeneyi ika ikawathandiza bwanji pa moyo wawo wa Uzimu?
- (5). Mukonzekere masewero osiyanasiyana. Kumbukirani kuti ana ang'ono amaphunzira msanga pakuchita zinthu kuposana ndi kumva. Pali zinthu zakuti muchite, paphunziro lililonse. M'maphunziro aja, a ana amene asanayambe sukulu, mudzaonjezerapo kufotokoza za zinthu izi.
- (6). Nthawi imene mwapangana kuti mudzikumana kapena nthawi yoyambira Sande Sukulu:
 - (a). Kulandira alendo mphindi 5.
 - (b). Kuyimba nyimbo ndi kuchita zina zonse.
 - (c). Kufotokoza nthano mphindi 10.

Muyenera kukhala ndi nthawi yokwanira mphindi 40-60 pa kalasi iliyonse. Muyenera kuyamba ndi kutsiriza nthawi yabwino. Ngati muli kukonzekera bwino maphunziro anu, mudzakhala ndi nthawi yabwino ndiponso ana adzaphunzira mokondwa.

- (7). Chinthu chofunika kwambiri. Muyenera kumafika kutchalitchi nthawi yabwino. Mphunzitsi ayenera kukonzekera malo ophunzilira. Muyenera kufika kutchalitchi mofulumira kuti mupatse moni mwana aliyense. Ichi ndi chinthu chofunika kwambiri.

7. SANDE SUKULU YAYAMBIKA

1. Tsiku la sabata lafika. Mwawerenga bwino, muli kudziwa zimene muphunzitse. Tsono mufike mofulumira ndi kuyamba kukonzekera malo pamene mumaphunzirirapo. Muyenera kuwakongoletsa malo amenewa. Mukhoza kuikapo maluwa ndi zithunzi.

Muphunzitse monga m'mene mwakonzekera ndipo muyenera kutsatira dongosolo limeneli.
2. Muyenera kugwiritsa ntchito zitsanzo pakuphunzitsa. Ana amafunika kuti asamagone pamene muli kuphunzitsa, mwa chitsanzo, muyenera kumawaimiritsa, kuomba m'manja, kuyenda ndi kuwakhazika pa mphasa.
 - (a) Kunena nthano kapena nkhani za m'Buku Lopatulika ndi gawo lalikulu ndipo lofunika kwambiri pakuphunzitsa. Musawerengere nkhaniyo anawo. Koma Buku Lopatulika likhale lotsegula, pamene muli kufotokoza nkhaniyo. Tsono, muyenera kukhala kuti muli kuidziwa nkhaniyo bwinobwino. Nkhani yake iyenera kukhala yaifupi. Mudziphunzitsa modekha ndi mofatsa ndipo mudzilankhula mawu akuti anawo adzimvetsetsa bwino. Ngati nkhani ija ikhala yokondweretsa, ana amamvetsera bwino ndipo amaphunzira mosabvuta.
 - (b) Ana amakonda masewero. Mukatha kufotokoza nkhaniyo, muwauze anawo kuti ayenera kufotokoza monga m'mene munachitiramo kapena achitenso sewerolo. Ngati aiwala muwakumbutse.
 - (c) Zooni ana amakonda kuyimba. Amaphunzira zinthu zambiri kupyolera m'nyimbo. Koma, muyenera kuona kuti anawo nyimboyo ali kuidziwa bwino pamodzi ndi mawu ake omwe. Pa chiswahili pali nyimbo ina imene anthu ambiri amaikonda. Amati, "Damu Yesu." Pa chichewa imatanthauza kuti "Mwazi wa Yesu." Ngakhale kuti ana akhoza kuyimba bwino nyimbo imeneyi, koma mawuwo amakhala opanda tanthauzo kwa iwo chifukwa samva zimene nyimboyo ili kunena. Buku lililonse limene aphunzitsi amalandira muli nyimbo zimene aphunzitsi akhoza kuphunzitsa ana. Zimenezi analembera ana ang'ono kuti adziphunzira. Tsono muyenera kuti mudziwaphunzitsa nyimbo zimenezi. Muyenera kuiphunzira nokha pamene musanayambe kuphunzitsa anawo.

- d. Muyenera kuwapatsa mpata wa kuyenda pa tchalitchi paja mwina kuti ayende m'magulu awiri kapena atatu. Inuyo muwatsogolere. Akhoza kukafuna maluwa, udzu kapena miyala. M'njira imeneyi amaphunzira bwino za chilengedwe cha Mulungu ndi m'mene Mulungu amasamalira dziko lapansi.
- e. Ena amakonda zonjambulajambula. Ngati muli ndi mapepala mukhoza kumawapatsa ana kuti adzijambula pamenepo. Ngati mulibe, mukhoza kugwiritsa ntchito makala ndi nyuzi pepala, kapena choko. Ana akhoza kumajambulira pansi. Koma mudziyesetsa kuwapatsa chinthu china kuti adzijambulirapo.

8. KUCHEZERA ANTHU

Chonde muwerenge mutu 6 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu. Ana a ang'ono sayenera kugawidwa m'magulu monga m'mene amachitira akulu ndi achinyamata. Inu, monga mphunzitsi wa Sande Sukulu, muyenera kumawachezera. Imeneyi ndi ntchito yofunika kwambiri. Kodi muli kukumbukira kuti ntchito yoyamba ya Sande Sukulu ndi chiyani? Ndi kuchitira umboni ana amene sabwera ku Sande Sukulu. Muwapemphe ngati angalole kuti ana awo adzibwera ku Sande Sukulu. Muyese kulimbikitsa mamembala a mumpingo mo kuti adzibwera ndi ana awo ku Sande Sukulu. Mudziphunzitsa ana osangoti kuwasamalira chabe. Muyenera kumawachezera kuti mukhale ndi ana ambiri pa kalasi yanupo.

Ntchito ina ndi kutumikira ana ndi mabanja awo onse. Kodi muli kukumbukira buku lija lolebapo maina a ana onse amene ali pa kalasipo. Muyenera kuchezera nyumba iliyonse kawiri pa chaka. Ngati mwana wina sabwera, ku Sande Sukulu sabata imeneyo, mupite kunyumba kwawo kukamuchezera. Mwina akhoza kukhala kuti ali kudwala kapena kunyumba kwawo kuli mabvuto ena. Umenewo ndi mwayi wanu wakuti muwathandizire.

Ana ang'ono sangathe kumvetsetsa za chipulumutso. Ndiponso ambiri makolo awo sanapulumutsidwe. Inu, monga mphunzitsi, muyenera kuwathandiza. Mukhoza kuwachitira umboni kuti alandire Yesu Khristu. Ichi ndiye cholinga chenicheni cha Sande Sukulu.

KUPHUZITSA ANA SANDE SUKULU

KUPHUZITSA ANA SANDE SUKULU

1. CHIKONZERO CHA MULUNGU PA ANA

1. Ana athu ndi tsogolo lathu.
2. Timasunga chuma ndi nthawi mwa iwo.
3. Ndi chinthu chofunika kuwaphunzitsa Mawu a Mulungu.
4. Kuphunzitsa ana ndi ntchito ya moyo wonse.
5. Mphunzitsi ayenera kumasonkhanitsa ana pamodzi ndi kumawaphunzitsa.

2. MAKHALIDWE A MPHUNZITSI

Mphunzitsi wabwino ndi munthu amene:

1. Amadziwa Yesu Khristu monga Mpulumutsi wake ndi Ambuye wa moyo wake.
2. Ambuye anamuitana kuti akhale mphunzitsi wa Sande Sukulu ndipo ali ndi mtima wokonda ana.
3. Ndi wokhulupirika ndi wodalilika.
4. Amadziwa kuchitira umboni ndi kutsogolera ana kwa Ambuye.
5. Amakonda kucheza ndi ana kunyumba kwawo.

3. M'MENE ANA AMAPHUNZIRIRA

1. Ana amaphunzira kupyolera nkumvetsera, kuwerenga, kuyang'ana ndi kuchita.
2. Ana amaphunzira mosiyanasiyana.
 - (a). Pakuzindikira okha.
 - (b). Kumvetsetsa.
 - (c). Zinthu zimene iwo amazidziwa kale.
 - (d). Kulankhula mobwerezabwereza kuti ana amvetsetse bwino.

4. CHIFUKWA CHAKE CHIMENE TIYENERA KUPHUNZITSA

- (1). Kuphunzitsa Buku Lopatulika.
- (2). Chipulumutso.
- (3). Kukula m'Chikhristu.

- (4). Kumvetsetsa kuti anthuwo ndi anthu ofunika.
- (5). Utumiki.

5. BUNGWE

- (1). Zaka.
- (2). Malo ophunzirira.
- (3). Nthawi.
- (4). Mabuku.
- (5). Kusintha makalasi.

6. KUPHUNZITSA ANA KUPYOLERA M'ZINTHU ZINA

- (a). Nkhani kapena nthano.
- (b). Masewero.
- (c). Zinthu zosiyanasiyana.
- (d). Kuwerenga.
- (e). Nyimbo.
- (f). Kulemba.
- (g). Zidole.
- (i). Nkhani za m'Buku Lopatulika.
- (j). Zonjambulajambula.
- (k). Mafunso pa zimene mwaphunzitsazo.

7. MAGAWO AMAPHUNZIRO

Gawo ndi gulu la maphunziro paphunziro limodzi. Zinthu zochitika ziyenera kukonzedweratu pa gawo lonse.

8. KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

- (1). Zinthu zimene muli kufuna.
- (2). Werengani gawo lonse.
- (3). Werengani ndime za m'Buku Lopatulika zimene ziri pamenepo.
- (4). Mulembe chikonzero chanucho pa kabuku kapena pa kope.

- (5). Mulembe chikonzero chanu sabata iliyonse.
- (6). Mulembe cholinga cha phunzirolo.
- (7). Musankhe sewero limene mudzachita.
- (8). Muwerenge bwino phunziro lanu limene lili mubuku la mphunzitsi.
- (9). Mudzikonzekera phunziro lililonse ndi zimene mukalankhula ndi kuchita pa kuphunzitsapo.
- (10). Nthawi yoyambira Sande Sukulu.
- (11). Mudzikonzekera kufika kutchalitchi nthawi yabwino.
- (12). Mukatsiriza kuphunzitsa, muonenso zimene mwaphunzitsazo.

9. KUCHEZERA ANTHU

Mphunzitsi ayenera kukachezera mwana aliyense kunyumba kwake. Umenewu ukhoza kukhalanso mwayi kuti mphunzitsi uja achitire umboni makolo a mwana uja pamodzi ndi abale ake onse

Werengani mutu 3 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

MAKALASI:

Ana aku mkaka.	Ana akulu pang'ono	Achinyamata	Akulu
-------------------	-----------------------	-------------	-------

Mwasankhidwa kukhala aphunzitsi ophunzitsa ana a Sande Sukulu. Aphunzitsi ena adziphunzitsa ana amene ali ndi zaka (7-9). Aphunzitsi ena adziphunzitsa ana akulupo amene ali ndi zaka 10-13. M'mipingo ina aziphunzitsi amaphunzitsa ana onse pamodzi. Pakuphunzitsa muyenera kukhala ndi buku limene munalembedwa zitsanzo ndi zithunzi-thunzi. Muyeneranso kuwerenga buku la aphunzitsi la Sande Sukulu.

1. CHIKONZERO CHA MULUNGU PA ANA

1. Ana ndi tsogolo lathu. Nthawi imene takhala tili kukhala nawoyi idzakhala nthawi yokolola zaka zili

kudzazi. Tiyenera kumakhala ndi chikonzero ndi ana athu, tiyenera kumawakonda, kumawaphunzitsa ndi kumawalimbikitsa. Tsono, zokolola zija zidzalemekeza Mulungu ndi kulimbikitsa anthu ena mumbado wanuwo.

2. Timaononga nthawi ndi ndalama zathu kuphunzitsa ana athu. Timadziwa kuti chinthu chofunika kuwaphunzitsa masamu, mbiri yakale ndi kuwerenga.
3. Ndi chinthu chofunika kwambiri kumawaphunzitsa ana Mawu a Mulungu. Kuphunzitsa ana Mawu a Mulungu ndi chinthu chofunika kwambiri. Mulungu amatiuza kuti tiyenera kudzaza maganizo a ana athu ndi miyoyo yawo ndi zinthu za Uzimu. Deuteronomo 6:5-8 timawerenga kuti, "Ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse. Ndipo Mawu awa ndikuuzani lero, azikhala pamtima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwachangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansi m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansi, ndi pouka inu. Ndipo muziwamanga padzanja panu ngati chizindikiro, ndipo akhale ngati cha pamphumi pakati pa maso anu."
4. Kuphunzitsa ana Mawu a Mulungu ndi ntchito yosatha osangophunzitsa pa sabata pokha. Ana asamangomva Mawu a Mulunguwa tsiku ndi tsiku, koma ayenera kumawasunga mawu amenewa. Masalmo 119:11 amati, "Ndinawabisa mawu anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire inu."
5. Kodi mphunzitsi amayambira kuti? Gawo lachiwiri la Deuteronomo 4:10 limati, "Ndisonkhanitsire anthu, ndidzawamvetsa mawu anga, kuti aphunzire kundiopa Ine masiku awo onse akukhala ndi moyo pa dziko lapanji, ndi kuti aphunzitse ana awo." Tiyenera kusonkhanitsa ana pamodzi. Sitingadalire kuti abwera okha kutchalitchi. Tiyenera kupita kunyumba kwawo, kuwaphunzitsa ndi kuwatsogolera kwa Ambuye. Werengani Mateyu 28:19-20. Ndime izi ndi zolimbikitsa kwambiri chifukwa zimatiuza kuti tiyenera kupita ndi kuwaphunzitsa ndipo Mulungu adzakhala nafe kuli konse kumene tidzapita.

2. MAKHALIDWE A MPHUNZITSI

Chonde muwerenge mutu 7, wa KUKULITSA TCHALITCHI KUPYOLERA SANDE SUKULU.

1. Mphunzitsi ayenera kukhala munthu amene amadziwa Yesu Khristu ndipo anamulandira kukhala Mpulumutsi wake ndi Mfumu ya moyo wake. Ayeneranso kukhala munthu amene ali chiwalo cha mpingo ndipo ndi munthu wokhulupirika. Ayenera kumaphunzira ndi kukula m'Chikhristu chake. Ayenera kukhala munthu amene amawerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera tsiku ndi tsiku. Ayenera kukhala ndi moyo wa chitsanzo.
2. Mphunzitsi ayenera kukhala munthu amene amamva kuti Mulungu anamuitana kukhala mphunzitsi. Ngati simuli kutsimikiza kuti Mulungu anakuitanani kuti mugwire ntchito imeneyi, tsono muyenera kuti mupemphere. Ngati Mulungu anakuitanani kuti mukhale mphunzitsi wa ana, muyenera kukhala ndi chikondi pa ana. Limeneli ndi khalidwe lofunika kwambiri kukonda ana.
3. Aphunzitsi ayenera kukhala ana okhulupirika ndi odalilika pa ntchito zonse za mpingo, osakhala kuphunzitsa Sande Sukulu kokha ayi. Mwana amaphunzira kukhala ngati mphunzitsi wake.
4. Mphunzitsi ayenera kuphunzira kutsogolera ana kwa Yesu. Ana ali ndi zosowa zosiyanasiyana; Mulungu amawalankhula m'njira zosiyanasiyana. Tsono, mphunzitsi ayenera kudziwa m'mene angawatsogolere kuti alandire Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wawo. Mphunzitsi ayeneranso kukhala munthu amene amadziwa kuchitira umboni wa Yesu Khristu kwa ana. Ayenera kuphunzira Mawu a Mulungu kuti aonetse anthu m'mene angapulumsidwire. Tsono, akhoza kutsogolera makolo ake ndi abale ake kwa Yesu Khristu.
5. Mphunzitsi ayenera kukhala munthu amene ali ndi moyo wa chitsanzo. Zinthu zimene mphunzitsi amachita pa kalasi yakeyo, monga kuwachezera ana aja, kuwathandiza kupeza choonadi cha Buku Lopatulika pa moyo wawo ndi kumawaphunzitsa kuwerenga Mawu a Mulungu ndi kumawakonda.
6. Mphunzitsi aliyense ayenera kumakachezera ana apa kalasi yake kunyumba kwawo. Ayenera kumawachezera nthawi zambiri. Nthawi zina ayenera kumatenga ana ena ndi kumayenda nawo pamene ali kuchezerana ana ena

Kunyumba kwawo. Adzaphunzira kuchezero anzawo ndi kuchitira umboni anthu ena.

Mphunzitsi kuti aphunzitse bwino ayenera kudziwa zosowa za ana amene ali pa kalasi yakeyo. Ayenera kufunsa Mulungu kuti amuthandize kukhala ndi chikondi chokonda mwana aliyense amene ali pa kalasi yakeyo. Kumbukirani kuti Yesu Khristu anaonetsa chikondi cha chifundo kwa munthu aliyense. Ngati mwana akadziwa kuti amakondedwa ndi aphunzitsi ake, amaphunzira msanga ndiponso saiwala zimene mphunzitsi ali kuphunzitsazo.

3. M'MENE ANA AMAPHUNZIRIRA

1. Aphunzitsi anapeza kuti ana amaphunzira ndi kumva 10%. Amawerenga 20%, amaona 50%, ndi zimene amachita 90%. Tsono, mphunzitsi wabwino amafuna kuti aphunzitse njira zambiri kuti athandize ana onse kumvetsetsa ndi kuphunzira bwino. Mphunzitsi adzafuna kuti ana aja adzimva, kuwerenga, kuona ndi kuchita zimene iye amaphunzitsazo. Chifukwa cha zimenezi tidzakhala tili kuchita zinthu zosiyanasiyana pa nthawi ya Sande Sukulu.
2. Pali magawo anai pa kuphunzira.
 - a. Choyamba, mwana amazindikira zinthu zatsopano. Zinthu zimene amaziona ndi kuzichita pa nthawi imeneyi, zambiri amaziwala.
 - b. Kachiwiri, mwana amamva zinthu zochitika. Ndipo amadziwanso tanthauzo lake.
 - c. Kachitatu, akhoza kuganizira chinthu ndipo ndikuganiziranso za tanthauzo lake ndipo zimene chinthucho chingapindule pa moyo wake.
 - d. Kachinai, akhoza kumva nkhani ndipo ndi kuigwiritsa ntchito pa moyo wake. Izi zimachitika pamene maphunziro aja aowadi m'moyo mwake. Izi ndi zimene tili kufuna kuti zidzichitika ndi Mawu a Mulungu amene tidzikhala tili kuphunzitsa.

4. CHIFUKWA CHA KUPHUNZITSIRA

Tikhoza kunena kuti cholinga cha Sande Sukulu ndi kuthandiza ana kuphunzira kuti akhale akhristu okhwima. Ana ali ndi zosowa zawo zimene zili zosiyanana ndi anyamata akuluakulu ndi anthu akuluakulunso. Timaphunzitsa ana pa Sande Sukulu kuti tiwathandize pa zosowa zawo za Uzimu.

1. BUKU LOPATULIKA - Ana ayenera kuphunzira choonadi cha Buku Lopatulika. Koma chofunika kwambiri ndi kuti ayenera kuthandizidwa kumvetsetsa tanthauzo la moyo wawo tsiku ndi tsiku. Tili kufuna kuti adzikhulupirira kuti Buku Lopatulika ndi loona, ndi kumakumbukira kupembedza ndi kupuma pa tsiku la sabata ndi kuphunzira kumvera malamulo a Mulungu.
2. CHIPULUMUTSO - Kuphunzitsa Buku Lopatulika kuyenera kuthandiza mwana aliyense kuti akhulupirire Yesu Khristu monga Mpulumutsi wake ndi Ambuye wa moyo wake. Mwana, pa nthawi ina, adzazindikira kuti ndi wochimwa ndipo ayenera kupulumutsidwa. Mphunzitsi wa Sande Sukulu ayenera kuwatsogolera ana kuti alandire Yesu Khristu.
3. KUKULA KWA MKHRISTU - Tili kufuna kuti mwana aliyense akule m'Chikhristu chake. Sande Sukulu ndiye maziko a kukula m'Chikhristu chake. Tili kufuna kuti akhale ana okhulupirika, kugwira ntchito ndi mphamvu ndi kumvera Buku Lopatulika.
4. KUFUNIKA KWAKE KWA ANA - Tili kufuna kuti ana amvetsetse kuti ali ndi gawo lalikulu pamaso pa Mulungu. Ana amafuna kuti mphunzitsi adziwalemekeza. Pamenepa ndi pamene amaphunzirira kuti ali ndi gawo lalikulu kwa mphunzitsi uja. Ndiponso ndi kwapafupi kwa iwo kuzindikira kuti ndi ofunika pamaso pa Mulungu.
5. UTUMIKI - Ana nthawi zambiri, amakonda kusewera ndi anzawo. Amaphunzitsana nyimbo, nthano ndi ndime za m'Buku Lopatulika zimene amaphunzira kutchalitchi. Timafuna kuti adzilemekezana ndi kuthandizana. Tikhoza kulemba zinthu zambiri. Pali nthawi yokwanira kuti tiphunzitse ana tsiku limodzi. Koma tikhoza kuona m'mene tingaphunzitsire ngati titawerenga bwino buku la Sande Sukulu, ndi cholinga chake pa sabata iliyonse. Mphunzitsi ayenera kumakhala wokonzeka bwino. Ayenera kuwerenga bwino gawo lililonse kuti adziwe bwino zimene akaphunzitse. Tsono, ayenera kukonzekera bwino tsiku la sabata lisanafike. Werengani mutu 3 pegi 12-14 pa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

(5). BUNGWE

Werengani mutu 5, pa KUKULITSA TCHALITCHI KUPYOLERA SANDE SUKULU.

1. ZAKA - Pa kalasi imeneyi ana ayenera kuti akhale ndi zaka 7-13. Ana amenewa ayenera kuti kusukulu ali kuphunzira sitandade 1-7. Sayenera kukhala ana oposa 20 pa kalasi iliyonse. Mukhoza kukhala ndi kalasi imodzi imene ili ndi ana amene ali ndi zaka 7-9 a kachisi amenewo, ndipo ana amene ali akulupo akhale ndi zaka 10-13. Muyenera kuona zaka za anawo kuti muone kalasi imene mungawaike.
2. MALC - Pa mutu 5 wa KUKULITSA TCHALITCHI KUPYOLERA SANDE SUKULU, werengani pegi 25-26. Ngakhale kalasi yanuyo ndi yomanga ndi njerwa kapena dothi, koma muyenera kuchitapo kanthu kuti idziona bwino.
 - (a). Mipando iyenera kuti ikhale yaifupi bwino kuti ana adzikhala mosabvutika. Ana akuluakulu akhoza kumakhala m'mipando m'mene amakhala nthawi zonse. Nthawi zambiri ana ang'onoang'ono amalongolola chifukwa sakhala bwino. Yesetsani kuti ana onse adzikhala pansi kuti adzikhala ndi nthawi yomvetsera bwino zimene mphunzitsi ali kuphunzitsazo. Mukhoza kukhometsa mipando kapena kuuza munthu kuti achite yomanga ndi njerwa koma iyenera kukhala yaifupi kuti ana akhoza kukhala bwino.
 - (b). Chotsatira, udziganizire wekha monga mphunzitsi. Uyenera kukhala pa mpando wofanana ndi mipando ya ana ija.
 - (c). Ngati muli ndi zithunzi, muzikhome pabwino kuti ana aja adziona bwino. Muyenera kusiya malo okwanira kuti ana aja adziyenda bwino ndi kutakasuka bwino.
 - (d). Pamalo pophunzirira paja, padziona bwino. Mudziikapo maluwa ndipo ngati pansipo pali fumbi mudziyalapo mphase.
 - (e). Ana ayenera kumakhala poyera kuti adziona bwino. Sibwino kuti ana adziphunzira m'nyumba imene ilibe mazenera kapena mwa mdima chifukwa amagona msanga.

3. NTHAWI - Mpingo uyenera kupangana nthawi yoyambira Sande Sukulu. Nthawi zambiri Sande Sukulu imayambika mofulumira pamene nthawi ya mapemphero isanayambike. Nthawi yophunzitsa iyenera kukhala mphindi 45-60. phunziro lililonse linakonzedwa kuphunzitsidwa pa nthawi imeneyi. Tsono, muyenera kuphunzitsa pa nthawi imeneyi ndi kutha nthawi yabwino.
4. MABUKU - Pa mabuku ambiri amene amapezeka ku I.P.S. okwanira kalasi iliyonse. Chonde werengani pa pegi 13-14 pa za KUKULITSA TCHALITCHI KUPYOLERA SANDE SUKULU. Chinthu chofunikira kwambiri ndi kukhala ndi maphunziro ophunzitsira okwanira kuti aphunzitsi adziphunzitsira.
5. KUSINTHA MAKALASI - Ichi ndi chinthu chofunika kwambiri kwa ana. Chaka chili chonse, sabata yoyamba ya January, muyenera kukonzanso makalasi. Ana ena amalowa kalasi ya ana akulupo, ana ena amayamba kumene. Siana onse amene amasintsha makalasi ena amakhala m'kalasi yomweyo zaka zambiri malinga ndi m'mene mpingo unganenere. Mwachitsanzo, pa tchalitchi yaing'ono, pakhoza kukhala makalasi awiri a ana. Kalasi ina ya ana ang'ono ndi kalasi ina ya ana akulupo. Ngati mwana woyamba sukulu, ayenera kuchoka pa kalasi ya ana ang'ono aja amene amapita ku mkaka aja ndi kulowa kalasi ya ana akulupo aja. Ngati mwana ali ndi zaka 13 kapena watsiriza sukulu ayenera kuyamba kalasi ya achinyamata akuluakulu ija. Chonde werengani mutu 5 wa za KUKULITSA TCHALITCHI KUPYOLERA SANDE SUKULU.

6. KUPHUNZITSA ANA KUPYOLERA M'MASEWERO NDI ZINTHU ZINA

Werengani mutu 3 pegi 12-14 pa za Kukulitsa Tchalitchi kupyolera Sande Sukulu.

Mutatha kuwerenga ndi kudziwa m'mene alili ana, mukhoza kudzifunsa funso ili, "Kodi ndikhoza kuchita chiyani pa ola lonseli pa sabata ngati ana sakonda kukhala pansi pa nthawi yaitali?"

1. Choyamba, mphunzitsi wa ana asakonzekere kuphunzitsa ola lachikhalire. Ana sangathe kumvetsera nthawi yonseyo. Ana amayamba kusewera kapena kulongolola chifukwa cha kutopa.

Mphunzitsi wabwino amakonzekera kuphunzitsa nthawi yochepa ndi kumawaphunzitsanso nthano za m'Buku Lopatulika. Ana amakonda kumva nthano ndipo ndiyo njira yapafupi yophunzitsira ana. Ana amafuna kuti adzimva nthano za m'Buku Lopatulika ndipo mphunzitsi ayenera

kuphunzitsa modekha bwino. Mphunzitsi ayenera kumalankhula pang'onopang'ono kuti ana aja adzimvetsetsa bwino. Osamalankhula mozungulira, kumalankhula momveka.

Ngati muli kuphunzitsa ana a zaka 7-9, pophunzitsa Mawu a Mulungu kapena nthano za m'Buku Lopatulika musaphunzitse kupitirira mphindi 10. Ana a zaka 10-13, mukhoza kuphunzitsa mphindi 15.

Mphunzitsi akamakonzekera kuphunzitsa ayenera kukonze-keranso masewero awiri kapena atatu. Ana aja pa Sande Sukulu paja amakhala pamodzi ndi kuchitira zinthu pamodzi.

Ngati muli aphunzitsi awiri, winayo athandizane ndi ana kuchita masewerowo. Ana akhoza kuthandiza pakuwerenga Buku Lopatulika kapena kukonza zithunzi. Ana akuluakulupo akhoza kuthandizana ndi anzawowo.

2. Pali zinthu zambiri zimene zikhoza kuthandiza ana kumvetsetsa ndi kukumbukira phunzirolo.

- a. Mukhoza kukonzekera mafunso. Akhoza kukonzedwa monga sewero. Ana aja akhoza kugawidwa m'magulu awiri kuti muone ndi gulu liti limene lingathe kuyankha bwino.
- b. Masewero oyenda pansi akhoza kukonzedwa ndi mphunzitsiyo ndi kulemba maina ana aja.
- c. Ana aja atatha kumvetsera nthano ya m'Buku Lopatulika ija, akhoza kubwereza ndi kuchita monga m'mene zinachitikira m'Buku Lopatulikalo.
- d. Ngati pali magulu awiri, gulu limodzi likhoza kuwerenga ndime zina ndiponso gulu linalo likhozanso kuwerenga ndime zinazo. Ana aja, pamene ena akuwerenga ana ena, akhoza kumalemba ndime za m'Buku Lopatulika.
- e. Mphunzitsi akhoza kulemba theka la ndime za m'Buku Lopatulika pa pepala ndi kupatsa ana aja, ndipo ayenera kupezanso theka linalo okha.
- f. Nyimbo ndi zofunika kwambiri kwa ana. Amakonda kuphunzira nyimbo zatsopano. Amakondanso kulemba nyimbo zatsopano. Mwana akaphunzira nyimbo imene mawu ake ali kufanana ndi zimene waphunzirazo saiwala msanga phunzirolo. Nyimbo imeneyi mukaibwerezabwereza ana saiwala ndipo amaphunzira msanga. Ana akhoza kupanga zipangizo za nyimbo kuti nyimbo zikhale bwino.

- g. Kulemba kumathandiza ana kuphunzira msanga. Ana amakonda kulemba ndakatulo. Ana akhoza kukhala m'magulumagulu ndi kumalemba ndime za m'Buku Lopatulika papepala m'mawu awoawo ngati nyuzi pepala.
- h. Ana akhoza kupanga zidole ndipo zikhoza kumagwiritsidwa ntchito pa nthawi yonena nthano. Akhoza kupanga ndi tinsaru kapena ndi mapepala. Ana akhoza kumaphunzira pang'onopang'ono mpaka atadziwa kusewera ndi zidole.
- i. Nkhani za anthu amene anali, kapena ali ndi chikhulupiro cha mphamvu zikhoza kuwapatsa mphamvu ndi kuwalimbikitsa ana.
- j. Kujambula zithunzi kukhoza kuthandiza ana kuti amvetsetse msanga zimene aphunzirazo. Ngati kuli kotheka, mukhoza kuwafunila mapepala kapena akhoza kumajambula pansi. Muyesere kuona m'dera lanulo zinthu zimene ana akhoza kumajambula. Akhoza kumajambula pansi ndi masekera kapena tindodo.
- k. Nthano za m'Buku Lopatulika ndi njira yofunika kwambiri kwa ana akuluakulu kuti azolowere msanga kuwerenga Buku Lopatulika. Mudziloweza ndime za pamtima ndi ndi mabuku amene ali m'Buku Lopatulika.
- l. Kutu muthandize ana kukumbukira bwino zimene aphunzirazo, muyenera kumawafunsa mafunso paphunziro lililonse limene mwaphunzitsa. Mutatha kuphunzitsa kuja, ana akhoza kumayankha mafunso amenewa pamodzi monga gulu. Sabata ikudzayi mukhoza kudzabwerezanso mafunso omwewo kuti muone ngati ali kukumbukira. Mukhoza kufunsa mafunso a maphunziro amene munaphunzitsa kale kuti muchite mpikisano.

7. MAGAWO OPHUNZITSIRA

Pamene mwatsiriza kuwerenga zinthu zimene muyenera kuchita mukhoza kufunsa funso ili, "Kodi munthu angathe kuchita zinthu zonsezi pa ola limodzi bwanji?" Zimenezi zimabweretsa gawo lalikulu pakuphunzitsa.

Masabata angapo pamaphunziro anu amene ali m'buku la aphunzitsi mwina akhoza kukhala okhudza phunziro limodzi.

Zimenezi zimatchedwa kuti gawo. Ndi chifukwa chake ndi kofunika kwambiri kwa inu monga mphunzitsi kuwerenga ndi kudziwa maphunziro amene amayendera pamodzi.

Mwachitsanzo, tiyeni tiyese kuti muli kuphunzira za zozizwitsa za Yesu Khristu sabata zinayi. Ngati ndinu wokonzekera bwino, mukhoza kuwathandiza ana kumvetsetsa m'mene phunziro ili lili kugwirizirana ndi ilo. Mudzakhozanso kusankha masewero ena ndi zinthu zina zochitachita ndi kudziwa kuti zingakutengereni sabata zingati kuti mutsirize.

8. KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

1. Tsopano, yakwana nthawi yakuti mukhale pansi ndi mabuku anu ndi kuyamba kukonzekera zimene mukaphunzitsazo. Muyenera kuti mukhale ndi zinthu zitatu: Buku Lopatulika, buku lophunzitsira la Sande Sukulu, ndi kope yanu kumene mudzilemba zimene mudzikonzekerazo.
2. Choyamba, muwerenge gawo la phunziro lanu lonse.
3. Muwerenge bwinobwino ndime zonse za m'Buku Lopatulika zimene zinalembedwa m'buku la aphunzitsi lija.
4. Mukope yanu ija mulembe dzina la gawo la phunziro limene mudzakhala muli kuphunzitsazo. Muganizire m'mene mukaphunzitsire phunziro lanulo. Mukonzekere masewero kuti akuthandizeni kuphunzitsa bwino ndi kuthandizanso ana kumvetsetsa bwino, kuti mukwaniritse cholinga cha phunzirolo.
5. Mulembe dzina la phunziro lililonse pamwamba pa pegi lililonse latsopano. Mukatha kulemba mutu wa phunzirolo mulembe kuti sabata loyamba, paphunziro linali mulembe kuti sabata yachiwiri mpaka mutafika potsiriza. Muyankhe mafunso awa pamene muli kukonzekera phunziro lililonse. Kodi ndikaphunzitsa bwanji? Kodi ndikayamba bwanji? Kodi ndikaphun ndikathanthauzira bwanji?
6. Muganizire cza cholinga chanu pa gawo limenelo. Kodi mukhoza kuligawa m'magulu ang'onoang'ono? Mulembe cholinga cha phunziro lililonse sabata iliyonse. Muyankhe funso ili, kodi ndikaphunzitsa chiyani? Mwachitsanzo, mukhoza kuti muli kuphunzitsa zozizwitsa za Yesu Khristu. Mukhoza kunena kuti cholinga chanu ndi kufuna kuphunzitsa ana kuti adziwe kuti Yesu amasamalira anthu ake m'zinthu zonse. Muyenera kuti mulembe cholinga chimenecho potsiriza pa gawo lanu lililonse.

Sabata yoyamba, mwina mukhoza kuphunzitsa za Yesu ali kuchiritsa munthu wakhungu. Mukhoza kuganizira kuti

cholinga chanu ndi chakuti muphunzitse ana kuti adziwe kuti Yesu amamva madandaulo a anthu amene amaitana Iye. Muyenera kulemba zimenezo pa pegi lachiwiri pamene munaiimba kuti "Sabata loyamba." Muchite zimenezi pa phunziro lililonse pa gawo lonse limene muli kuyembekezera kukaphunzitsa. Zolinga zanu zonse pamodzi ziyenera ku kukuthandizani kukwaniritsa cholinga cha gawo lonse.

7. Chinthu china chofunika ndi kusankha zinthu zophunzitsira monga zithunzi ndi zidole. Muwerenge m'buku la aphunzitsi kuti muone zinthu zimene analemba zokuthandizani pakuphunzitsa, musankhe zinthu ziwiri kapena zitatu. Musankhe zinthu zimene muli kudziwa kuti zikhoza kuthandiza ana kumvetsetsa bwino phunziro limene muli kuphunzitsalo. Muganizirensa za zinthu zimene zikhoza kukuthandizani kuti ana aja amvetsetse ndithu monga mapepala ndi zina zotere.
8. Muyenera kuliwerenga kwambiri phunziro limene muli kuyembekezera kukaphunzitsalo. Muyenera kudziwa bwino nkhanayo kuti ngati muli kufuna kuuza munthu wina mukhoza kumuza osayang'ananso pa buku paja. Muyenera kukonzeka bwino musanafike pa kalasi paja. Muyenera kuyesera kudziphunzitsa nokha kuti mudziwe bwino zimene mukalankhule pophunzitsapo. Ngati phunziro lanulo ndi lalitali muyesetse kulifupikitsa.
9. Mudzikonzekera bwino chinthu chili chonse. Chimene mukanene ndi kuchita kumeneko. Mukonzekere bwino nyimbo zimene mukayimbe kumeneko. Muyenera kudziwa ndime za m'Buku Lopatulika zimene mufuna kuti mukawerenge. Muloweze pamtima ndime zonse za pamtima. Muone kuti mwayankha mafunso ali pa mutu 5 aja.
10. Nthawi yoyambira Sande Sukulu.

(a). Kulandira alendo	mphindi 5.
(b). Kubwereza zinthu za sabata yathayi	mphindi 5.
(c). Phunziro	mphindi 15.
(d). Zochitika	
11. Pa tsiku la sabata m'mawa muyenera kufika mofulumira; mukonze bwino pa malo paja. Mudzipatsa moni mwana aliyense pamene ali kufika. Muyambe nthawi yabwino ndi kutsirizanso nthawi yabwino. Pemphererani Mzimu Woyera kuti akutsogolereni.

12. Mutatha kuphunzira, mudzifunse nokha, kuti muone zimene munachita bwino ndi zimene simunachite bwino.

KUCHEZERA ANTHU

Werengani mutu 6 za KUKULITSA TCHALITCHI YANU KUPYOLERA SANDE SUKULU.

"Cholinga cha Sande Sukulu ndi kusunghanitsa anthu a mumpingo kuti achitire umboni anthu amene ali m'dera lawo." Ntchito ina yaikulu kwa aphunzitsi a ana ndi kuphunzitsa ana kuwerenga Mawu a Mulungu ndi kuwalimbikitsa kuti adzibwera kudzapahunzira Mawu a Mulungu kamodzi pakati pa sabata. Pamenepa ndiye kuti Sande Sukulu yanu idzakhala ndi ana a zaka 7-13. Anthu ena amapita ku mipingo ina, koma ena sapita kutchalitchi, amangokhala. Mupite kunyumba kwawo ndi kukacheza nawo. Muyese kuwaitana kuti abwere kutchalitchi kudzapemphera nawo. Mupemphe makolo awo ngati angalole kuti ana awo abwere ku mpingo wa Baptist.

Ntchito ina ya mphunzitsi ndi kuchitira umboni kwa ana ndi mabanja awo. Ngati mwana sanabwere ku Sande Sukulu, mupite kunyumba kwawo kuti mukamuone ndi kumufunsa kuti mudziwe chifukwa chake sanabwerere ku Sande Sukulu. Ngati pali bvuto mwina mukhoza kuthandizana naye.

Ntchito ina yofunika kwambiri ndi kuwatengera kwa Yesu Khristu. Mwana amene ali ndi zaka 10-13 amadziwa bwino Mawu a Mulungu. Akhoza kudziwa tchimo. Kupyolera nkuwerenga Buku Lopatulika ndi kuliphunzira ana akhoza kudziwa kuti Yesu akhoza kuwakhululukira machimo awo. Muyese kucheza ndi mwana aliyense ndi kulankhula naye pa yekha. Ngati Mzimu Woyera ali kukutsogolerani, muyese kumuuza m'mene munthu amapulumsidwira.

Mudzifunse nokha, "Zinthu zimene sizili kuchitika, koma mufunika kuti muyambe kuzichita." Kodi mumacheza nawo ana amene mumawaphunzitsawo? Kodi mumawachitira umboni?

Mphunzitsi wabwino ndi amene nthawi zonse amafuna kuti apeze njira zopitilizira maphunziro ake. Muwerenge buku la Sande Sukulu la aphunzitsi, gawo la ana ndi KUKULITSA TCHALITCHI YANU KUPYOLERA SANDE SUKULU.

**KUPHUNZITSA ACHINYAMATA SANDE
SUKULU**

KUPHUNZITSA ACHINYAMATA SANDE SUKULU

1. ZOFUNIKA PAKUPHUNZITSA ACHINYAMATA BUKU LOPATULIKA

1. Zimawathandiza kukhala ndi maziko pa kusankha ndi kuchita zinthu.
2. Zimathandiza achinyamata kupeza malonjezo a Mulungu pa miyoyo yawo.
3. Zimawalimbikitsa, kuwaphunzitsa ndi kuwathandiza kuti adzitumikira.
4. Zimaonetsa chikondi cha Mulungu kwa anthu otayika pamodzi ndi akhristu.
5. Zimathandiza achinyamata kuti akhale ndi makhalidwe owerenga Mawu a Mulungu.

2. MAKHALIDWE A MPHUNZITSI WABWINO

1. Ayenera kukhala munthu amene anapulumutsidwa ndi chiwalo chimodzi cha mpingo wa Baptist.
2. Ali ndi luso la kuphunzitsa.
3. Ndi mkhristu wokhwima amene amawerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera tsiku ndi tsiku.
4. Ndi wodzipereka kuphunzitsa achinyamata; amakondwera kukhala ndi achinyamata.
5. Amabwera ku Sande Sukulu sabata ndi sabata.

3. ZOFUNA ZA ACHINYAMATA

1. Wokondedwa ndi anthu ndi anzako omwe kapena wobvomerezedwa ndi anthu ndi anzako.
2. Munthu amene angathe kusamala udindo wake.
3. Anachita maphunziro a udindo.

4. ZOKONZEKERA ZA MPHUNZITSI

1. Kukonzekera.
(a). Kupemphera.

- (b). Kuwerenga Buku Lopatulika.
- (c). Kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika.
- 2. 2. Kukonzekera phunziro.
 - (a) Muwerenge ndime zonse za m'Buku Lopatulika zimene zili pa phunziropo.
 - (b) Muwerenge phunziro lonse bwinobwino pamodzi ndi mabuku ena amene angakuthandizeni kuti mukonzekere bwino.
 - (c) Mulembe phunziro lanu ndi m'mene mukaphunzitsire.
 - (d) Musankhe njira za kaphunzitsidwe kamene kangathandize kalasi yanu kuphunzira bwino.

5. ZINTHU ZOPHUNZITSIRA

- 1. Ana aja adzikhala m'magulu ang'onoang'ono kuti adzithandizana mabvuto awo amene ali kuwapeza pa Sande Sukulu kapena kunyumba.
- 2. Zinthu zophunzitsira.
- 3. Kaphunzitsidwe.
- 4. Sewero.
- 5. Kuphunzitsa.
- 6. Kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika.
- 7. Kukambirana pa gulu.
- 8. Kumvetsera zimene magulu ena ali kuchita.
- 9. Masewero.
- 10. Maumboni.

6. MAKONZEDWE AKE

- 1. Zaka; kukula kwake kwa kalasiyo.
- 2. Malo ophunzirirapo.
- 3. Nthawi yoyambira.
- 4. Mabuku ophunzirila.
- 5. Kusintha kwa makalasi.
- 7. Mphunzitsi amene sayenera kungochezera achinyamata amene amabwera ku Sande Sukulu okha, komanso ayenera kumachezera achinyamata amene sabweranso ku Sande Sukulu.

Pali magulu anayi a Sande Sukulu.

1	2	3	4
Kalasi ya ana amene asanayambe sukulu	ana amene anayamba sukulu.,	Achinyamata	Akulu

Werengani mutu 3 wa Kukulitsa Sande Sukulu Kupyolera Sande Sukulu. Mwasankhidwa kuti muphunzitse aphunzitsi ophunzitsa Sande Sukulu ya achinyamata.

Pa gulu la achinyamata pali magulu awiri, gulu la zaka 13-15 ndi zaka 16-20. M'matchalitchi ang'onoang'ono magulu amenewa akhoza kuphatikizana ndi kukhala gulu limodzi.

Zaka zapitazi matchalitchi anazindikira za kuchuruka kwake kwa achinyamata pa dziko lapansi pano. Mu Afirika muno muli achinyamata ambiri. A Baptist ayenera kupeza njira zabwino zochitira umboni kwa achinyamata amenewa. Njira ina yabwino ndi kuwachitira umboni kupyolera pa Sande Sukulu. Ichi chitanthauza kuti tiyenera kuphunzira njira zotukulira Sande Sukulu ndi kumachezera anthu. Mwanjira imeneyi tiyenera kuphunzira makhalidwe a mphunzitsi wabwino wa Sande Sukulu wa achinyamata, zofuna za achinyamata, kufunika kwake kwa kuphunzitsa Buku Lopatulika pa moyo wa achinyamata ndi njira zina zophunzitsira zimene zingathe kuthandiza achinyamata kuti aphunzire bwino.

KUFUNIKA KWAKE KWA KUPHUNZITSA BUKU LOPATULIKA ACHINYAMATA PA MOYO WAWO

Pali mabvuto akulu kwambiri pa moyo wa achinyamata. Iyi ndi nthawi imene munthu ali kusintha pa moyo wake. Ndi nthawi imeneyi imene tiyenera kuphunzitsa Buku Lopatulika. Achinyamata ayenera kudziwa kuti Mulungu amafuna kulankhula nawo nthawi iliyonse imene ali kuwerenga Buku Lopatulika.

1. Zinthu zimene achinyamata amaganizira ndi kuchita ziyenera kumachokera m'Buku Lopatulika. Mphunzitsi ayenera kumaphunzitsa zimenezi pa Sande Sukulu ndi kuwathandiza m'mene angapezere choonadi m'Buku Lopatulika ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo wa Chikhristu. Buku Lopatulika limathandiza pa nthawi ya mabvuto, ndiponso limatipatsa nzeru pamene tiri kuthandiza anthu.

2. Buku Lopatulika limatiphunzitsa achinyamata malonjezano a Mulungu. Zimawathandiza kuti asinthe m'moyo wawo.
3. Ndikofunika kwambiri kuti achinyamata adziwerenga Buku lopatulika. Zimawalimbikitsa, ndipo zimawaphunzitsa kuti akhale adindo. Sande Sukulu ndi yofunika kwambiri kwa akhristu atsopano chifukwa ndi malo wokhawo amene angapeze maphunziro a moyo wa Chikhristu.
4. Buku Lopatulika limaphunzitsa achinyamata za chikondi cha Mulungu chosasinthika ndipo kuti Mulungu amawakonda. Zimenezi ndi zofunika kwambiri kuti achinyamata azidziwa kuti Mulungu amawakonda. Mphunzitsi ayenera kumawaonetsa achinyamata chikondi cha Mulungu chimenechi. Chikondi cha Mulungu chikhoza kudziwika ngati anthu achionetsa kwa anzawo.
5. Achinyamata ayenera kumakhala pamodzi ndi kumaphunzira Mawu a Mulungu kumawathandiza kuti adzikhala ndi mtima wokhala pamodzi ndi kumaphunzitsana Buku Lopatulika.

Werengani mutu 1 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

2. MAKHALIDWE A APHUNZITSI ABWINO

Tchalitchi iliyonse iyenera kudziwa kuti achinyamata ndi atsogoleri am'tsogolo. Chifukwa cha chimenechi tchalitchi iyenera kukhala ndi gawo lalikuru pa kuphunzitsa gulu limeneli. Achinyamata akakumana ndi mphunzitsi wabwino, nawonso amadzakhala atsogoleri abwino ndiponso amphamvu, tsono ndi chinthu chofunika kuti tchalitchi iliyonse iyenera kusankha anthu abwino ndi amphamvu kuti akhale aphunzitsi achinyamata.

1. Mphunzitsi ameneyu ayenera kuti akhale munthu amene anapulumsidwa ndipo ndi chiwalo chimodzi cha mpingo wa Baptist. Ayenera kuti ali kudziwa bwino malamulo a mpingo wa Baptist. Adzakhala ali kuphunzitsa achinyamata za chipulumutso, chikhulupiriro cha mpingo wa Baptist ndi makhalidwe a mkhristu.
2. Mphunzitsi wa achinyamata ayenera kukhala kuti ndi munthu amene ali ndi mphatso ya uphunzitsi ndipo ndi munthu amene amakonda kuwerenga. Ayenera kukhala munthu wofuna kuphunzira. Achinyamata sakhutitsidwa ndi maphunziro a Buku Lopatulika lokha ayi. Amafuna kudziwa m'mene Buku Lopatulika lingawathandizire pa moyo wawo ndi mabvuto awo a tsiku ndi tsiku.

3. Mphunzitsi wabwino ayenera kukhala mkhristu amene ali wokhwima. Ichi chimatanthauza kuti simkhristu watsopano, ndi munthu amene wakhala wokhulupirika m'matchalitchimo pa nthawi yaitali. Mkhristu wokhwima ndi amene amawerenga Buku Lopatulika lake ndi kupemphe-
ra tsiku ndi tsiku. Amachitira umboni anthu ena. Amauza anthu ena m'mene angapulumutsidwire. Munthu ameneyu ayenera kumadzipereka ku nthawi yophunzira Buku Lopatulika, kuchezera anthu ndi kuthandiza ACHINYAMATA amene pa kalasi yake ali ndi zosowa zawo za Uzimu.
4. Mphunzitsi ameneyu ntchito yake ndi kuphunzitsa achinyamata. Ayenera kumakondwera nawo udindo ndipo ayenera kumakonda kukhala ndi achinyamata ndi kumasewe-
ra nawo pa nthawi imene ali ndi masewero awo. Ayenera kukhala munthu amene ali ndi makhalidwe amene achinyamata adzakondwera nawo monga mphunzitsi wawo. Kumbukirani kuti ana amaphunzira kwambiri zinthu zimene mumachita kuposana ndi zimene mumalankhula.
5. Munthu ameneyu ayenera kukhala kuti amabwera ku Sande Sukulu nthawi zonse. Anthu asasankhe munthu amene sabwera ku Sande Sukulu ndi kuganizira kuti akakhala mphunzitsi mwina adzayamba kulimbikira.

Izi ndi zinthu zina zofunika kwa mphunzitsi wophunzitsa achinyamata. Werengani mutu 7 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

3. ZOSOWA ZA ACHINYAMATA

Achinyamata ali ndi nthawi yosintha ndi nthawi yotukuka. Achinyamata amakula mpaka kukalamba. Siana ndiponso sanafike pokula. Achinyamata ali ndi zosowa zawo molingana ndi nthawi ndi makhalidwe awo. Mphunzitsi ayenera kuzindikira zimenezi.

1. Anyamata amafuna kuona kuti alandiridwa bwino. Amafuna kuti akuluakulu adziwabvomereza zimene ali kuchitazo. Amafuna kuti adzikhala pamodzi ndi akuluakulu. Amafuna kuti adzifanana ndi anzawo. Amafuna kuti adzikondedwa ndi anzawo.
2. Ngakhale kuti anyamata sanafike pa msinkhu wa munthu wamkulu, koma amafuna kuti adzikhala ngati munthu wamkulu. Akhoza kuchita ntchito ina imene akuluakulu amagwira. Ndi chinthu chofunika kuti akuluakulu azidziwa gawo limene achinyamata akhoza kuchita m'tchalitchi. Akhoza kuyimba pa kwaya, akhoza kuchezera anthu ndi kuchitira umboni. Anyamata a Sande Sukulu ali ndi mwayi okhala atsogoleri pakati pawopo.

3. Achinyamata akhoza kuphunzira. Amafuna kuphunzira. Amabwera ku Sande Sukulu chifukwa amafuna kuphunzira. Achinyamata amafuna kuphunzitsidwa m'mene angagwiritsire ntchito Buku Lopatulika pa moyo wawo.

Mphunzitsi ayenera kuwathandiza pa zosowa zawo zimenezi. Kaphunzitsidwe kameneka kadzafunika kuti achinyamata aja akachitire umboni kwa anthu ena m'madera osiyanasiyana. Mphunzitsi ayenera kumawachitira umboni anyamata aja. Ayenera kumakhala ndi nthawi yocheza nawo anyamata aja ndi kukhala nawo pamodzi pa nthawi ya masewero ndi chiyanjano. Mphunzitsi amene amaphunzitsa chotere akhoza kuthandiza achinyamata kwambiri ndiponso mpingo ukhoza kukhala ndi tsogolo labwino.

Werengani mutu 3 pegi 14-15 Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera m'Sande Sukulu.

4. KUKONZEKERA KWA MPHUNZITSI

Mphunzitsi kuti aphunzitse Sande Sukulu bwino ayenera kuti akonzekere bwino sabata iliyonse. Mphunzitsi ayenera kutsatira zinthu izi kuti atsimikizedi kuti wakonzekeradi phunziro lililonse.

1. KUKONZEKERA - Mphunzitsi poyamba ayenera kukonzekera moyo wake kuti alandire Mawu a Mulungu.

- (a). Pemphero ndiye chinthu choyamba ndiponso gawo loyamba. Ayenera kuti afunse Mulungu kuti amvetsetse bwino zoonadi za m'Buku Lopatulika zimene Mulungu ali kufuna kuti iye aziphunzitse. Mphunzitsi ayenera kuti afunse Mulungu kuti athandize achinyamata kuti amvetsetse choonadi chimene Mulungu ali kuwasungira iwo. Mphunzitsi ayenera kupempherera aliyense ndi kumamutchula dzina lake. Pemphero ndi gawo lalikuru pakukonzekera phunziro lathu. Zimenezi nthawi zambiri, zimaiwalika, koma ndi gawo limeneli limene limasiyanitsa pakati pa maphunziro aku sukulu ndi maphunziro a Mawu a Mulungu.
- (b). Mudziwerenga ndime zonse za m'Buku Lopatulika zimene ziri pa phunziropo sabata ndi sabata. Kuwerenga ndime za m'Buku Lopatulika kumathandiza mphunzitsi kuti azindikire zoonadi za m'Buku Lopatulika.
- (c). Muloweze mawu apamtima. Mphunzitsi ndi chitsanzo cha ana aja amene ali kuwaphunzitsawo. Muyenera kuloweza ndime ya pamtima kuti achinyamata aja aphunzire kufunika kwake kwa kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika. Komanso ndime ya pamtima ija nthawi zambiri imakhala ndime yaikulu paphunziro lija.

2. KUKONZEKERA PHUNZIRO

- (a). Lowezeni ndime zonse za pamtima zimene ziri pa phunziropo. Ndi chinthu chofunika kwambiri kuti mphunzitsi adziwadziwa bwino Mawu a Mulungu ndi kumawaloweza pamtima. Pamene muli kuphunzitsa muone kuti muyenera kuphunzitsa zimene ziri pamenepo ndipo zimene ndime za m'Buku Lopatulikazo ziri kunena. Pakuwerenga Mawu a Mulungu mphunzitsi ayenera kumafunafuna ndime za m'Buku Lopatulika zimene ziri ndi malonjezano a Mulungu ndi njira zake zolandilira malonjezanowo. Mawu amenewa ndi awa "ngati," "koma," "komabe," "pamene." Izi ndi zinthu zimene Mulungu anaika kuti zikhale zizindikiro zathu zolandilira malonjezano. Aphunzitsi amaiwala kuti malonjezano ambiri, Mulungu anauza akhristu zimene ayenera kuchita kuti alandire malonjezanowo. Mwa chitsanzo pa 2 Mbiri 7:14, Mulungu anati, "Ngati anthu anga otchedwa dzina langa akadzichepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zawo zoipa; pamenepo ndidzamvera m'mwamba, ndi kukhululukira choipa chawo, ndi kuchiritsa dziko lawo." Liwu lakuti "ngati" litsimikiza kuti pali zizindikiro ndipo pali zinthu zofunika kuti munthu achite. Zinthu zake zakuti munthu achitezo ndi izi, kumvera, kupemphera ndi kudzichepetsa. Ngati munthu sangathe kukwaniritsa zimenezi, tsono Mulungu sangathenso kukwaniritsa malonjezano ake. Muloweze ndime imeneyi ndi imene mphunzitsi ayenera kuiloweza pa phunziropo.
- (b). Muwerenge phunziro lonse ndi mabuku onse ophunzitsira. Muwerengenso mitu yonse ya zigawo. Chigawo ndi magulu a maphunziro amene ali pa mutu umodzi. Mutu wa phunzirowo ndi umene ukuuzeni zimene ziri m'phunzirolo. Ndime ya pamtima ndi imene imafotokozaza chofunika cha phunzirolo. Ndipo ndime za Buku Lopatulika zimene ziri pa phunziropo ndi zimene zikufotokozereni chofunika chenicheni cha phunzirolo. Muyankhe funso ili: Kodi ndili kufuna kuti anthu awa aphunzire chiyani pa phunziro ili? Muwerenge mafunso onse amene ali potsiriza pa phunziro lililonse; mphunzitse bwino kuti potsiriza akhoza kuwayankha bwino mafunso aja.
- (c). Mulembe chikonzero chanu cha phunziro lililonse pamene muli kukonzekera kukaphunzitsa. Mulembe zimenezi mukope yanu. Kodi muyamba bwanji? Muyenera kukhala ndi chidwi cha kuphunzira ndi kumvetsera. Mugwiritse ntchito nkhanu yokondweretsa kapena chinthu china chimene chingakondweretse anthu ndi kuwachititsa chidwi.

Chachiwiri, muwerenge ndime za m'Buku Lopatulika zimene zili pa phunziropo. Muwerengere pamodzi, muuze anthu awiri kuti awerenge ndime zija. Muwathandize anthu aja kupeza tanthauzo lake la ndime iliyonse kapena mutu wonse uja. Kodi analembela yani ndipo analemba kwa ndani ndipo cholinga chake ndi chiyani?

Tsono, muone m'mene muwathandizire anyamata aja ndi zimene Mawu a Mulungu ali kunena. Amafunika kuti adziwe m'mene Mawu a Mulungu angawasinthire moyo wawo.

- d. Tsono musankhe njira za kaphunzitsidwe kamene kangathandize kalasi yanuyo kuti iphunzire msanga. Mulembe njira imene musankheyo pa phunziro lililonse. Mugwiritse ntchito njira zosiyanasiyana.

Chinthu chotsalira ndi kufotokoza njira zosiyanasiyana za kaphunzitsidwe. Aphunzitsi ayenera kusankha njira zosiyanasiyana zimene zidzakwaniritsa zosowa za achinyamata ndipo ayenera kuphunzitsa zinthu zofunikira zimene zili pa phunziro lililonse.

5. KUPHUNZITSA ZINTHU ZOCHITIKA

1. Kuthandiza mabvuto ang'onoang'ono amene amakhala pa gulupo. Gulu lalikulu la achinyamata likhoza kugawidwa m'magulu awiri kapena anayi. Gulu lililonse liyenera kupatsidwa funso lakuti liyankhe. Patapita nthawi magulu ali onse ayenera kubwera pamodzi ndi kufotokoza zimene agwirizana pa gulu lawolo. Mwachitsanzo: Funso likhoza kukhala motere, "Kodi tikhoza kuloweza bwanji Mawu a Mulungu? Mugawe kalasiyo m'magulu awiri. Ngati kalasi yanu ili ndi achinyamata 24, muwagawe m'magulu anayi ndipo pa gulu lililonse padzikhala anthu 6.

Muwathandize zinthu izi:

GULU LOYAMBA: Tiyese kuti muli kundende ndipo mulibe Buku Lopatulika. Ndipo mufuna kuti muloweze pamtima ndime za m'Buku Lopatulika. Mulembe njira zake zimene mungalowe-zere Mawu a Mulungu.

MAYANKHO:

- (a). Mufunse Mulungu kuti akuthandizeni.
(b). Mufunse akaidi anzanuwo kuti anene ndime ya m'Buku Lopatulika imene amaidziwa.
(c). Ndi ndime zimenezo mupange nyimbo ndipo mudziimba.
(d). Mutenge pensulo ndi pepala, kapena choko ndi kulemba ndime za m'Buku Lopatulikalo pa chipupa kapena pansi.

GULU LACHIWIIRI: Anthu akuluakulu nthawi zambiri amati sangathe kuphunzira Mawu a Mulungu. Ntchito yanu ndi kuwaonetsa kuti akhoza kuphunzira ndipo palibe chinthu chobvuta.

MAYANKHO:

- (a). Muphunzire ndime zambiri za m'Buku Lopatulika; muwaphunzitse ndi chitsanzo.
- (b). Muwafunse kuti akuuzeni ndime ya pamtima imene amaikonda.
- (c). Mulembe papepala kapena pa bolodi ndime ya pamtima ya sabata iliyonse. Muibwereze sabata iliyonse.
- (d). Muwaphunzitse m'mene angaloweze ndime ya pamtima.

GULU LACHITATU: Muli kufuna kuti mukhale mkhristu wamphamvu, koma mumapeza mabvuto pakuloweza Mawu a Mulungu. Kodi gulu limeneli likhoza kuganiza chiyani?

MAYANKHO:

- (a). Muwerenge Mawu a Mulungu nthawi yaitali.
- (b). Mulembe ndime za m'Buku Lopatulika papepala, muliike pa tembulo pamene mumadyerapo. Mudziwerenga nthawi iliyonse pamene muli kudya.
- (c). Muwerenge ndime za m'Buku Lopatulika katatu musanagone.
- (d). Muyimbe nyimbo ya ndime za m'Buku Lopatulika monga Masalmo 23.

GULU LACHINAYI: Muli ndi ana amene sangathe kuwerenga? Kodi akhoza kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika bwanji?

MAYANKHO:

- (a). Mudziwerenga nthawi ndi nthawi.
- (b). Munene pamodzi nthawi yaitali.
- (c). Mudzitenga ndime za pamtima zazifupi. Mupitirize mpaka ataphunzira ndime yonse ija.
- (d). Mupeke nyimbo zambiri kuti ziwathandize kuloweza Mawu a Mulungu.

2. BUKU LOPHUNZITSIRA

Buku Lophunzitsira ndi m'mene analemba njira za kaphunzitsidwe ndipo ndi m'mene analembamo maphunziro osiyanasiyana. Kalasi imagawidwa m'magulu awiri kapena

atatu. Gulu lililonse liyenera kugwiritsa ntchito Buku Lopatulika kuti apeze bwino mayankho a mafunso amene ali kuyembekezera kuti ayankhewo. Mukhoza kuchita sewero kuti mphunzitsitse bwino, kapena tepi imene ili ndi nkhani yokondweretsa. M'maphunziro a Sande Sukulu m'mene muli zinthu zenizeni, ana kapena akuluakulu amatha kuphunzira kuchita zinthu pa okha.

Mwachitsanzo: Mwana wa sukulu ali kukonzekera kulemba mayeso. Mnzake afuna kumupatsa mapepala a mayeso akale. Tiyese kuti munali inuyo mkhristu tafotokozani m'mene mukadachitira. Pakuyankha funso limeneli, mulembenso ndime za m'Buku Lopatulika kutsimikiza yankho lanulo. Muyenera kuwapatsa nthawi yokwana mphindi 5-10. Gulu lililonse lidzanena mayankho awo pamodzi.

3. CHIONETSERO

Iyi ndi njira imodzi yamphamvu ya kaphunzitsidwe. Sikungophunzitsa kokha, koma imaonetsa anthu m'mene munthu angachitire chinthucho. Mwachitsanzo: Phunziro la kuchitira umboni. Mphunzitsi ndi anthu amene ali pa Sande Sukulu paja adzaonetsa anthu m'mene angachitire umboni. Kalasi ija ikhoza kukambilana zimene zinachitika. Ngati pali nthawi mugawe kalasi ija m'magulu awiri kapena atatu ndi kuyeseranso kuchita zimene anazionazo.

4. SEWERO

Sewero limafunika anthu ambiri komabe mwina akhoza kuchita munthu m'modzi. Pamakhala pepala pamene analemba phunziro limeneli. Pamenepa anthu amene ali kuchita sewero aja ayenera kukonzekera pamodzi ndi mphunzitsi uja. Ngati mutachita bwino, zidzathandiza anthu kwambiri ndipo sadzaiwala msanga.

Mwachitsanzo: Sabata linalo, tsiku la paskha lisanaſike, mphunzitsi akhoza kuwerenga mokuwa, kuchita ngati muja anali kuchitira wa Chiroma uja amene anali kuthandizira pa nthawi ija pamene Ambuye Yesu anali kupachikidwa pamtanda paja. Zikhoza kuoneka ngati kuti Msirikali wa Chiroma uja anali kuuza mnzake zinthu zimene ziti zichitike pa tsiku lililonse. Njira imeneyi ndi yabwino kwa mphunzitsi amene amatha kukonza masewero ndi zinthu zina pamodzi ndi kalasi yake.

5. KUPHUNZITSA

Kuphunzitsa ndi njira imodzi yabwino imene anthu ambiri amaigwiritsa ntchito pakufotokoza zinthu. Mwinanso ndi

gawo lalikulu limene anthu ambiri satha kuligwiritsa ntchito bwino. Phunziro likhoza kukhala kuti sali kulimva bwino ndipo nthawi zambiri mphunzitsi sadziwa ngati anthu aja amvetsetsa bwino kapena ayi.

Pakukachezera anthu amenewa mudzipita ndi anthu ena amene ali pa kalasipo. Mphunzitsi ayenera kuwaphunzitsa anthu amenewa kuchitira umboni ndi kuchezera anthu. Kumbukirani kuti achinyamata amafuna kuti mudziwapatsa ntchito yakuti achite. Tsono, ndi chinthu chofunika kuti pamene muli kupita kukachitira umboni ndi kukachezera anthu, mudziwatenga achinyamatawa.

Muwerenge mutu 6 wa Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

Pa nthawi ya kuphunzitsa, mphunzitsi akhoza kuphatikiza ndi njira zina za kaphunzitsidwe kuti anthu amvetsetse bwino.

Mwachitsanzo: Ngati mbusa ali kulalikira kapena kuphunzitsa, amalalikira mphindi 30. Ngati ana aja kapena anthu aja ali ndi mafunso, amaiwala kuti afunse. Phunziro likhoza kukondweretsa ngati ana aja aloledwa kuti adzifunsa pamene phunziro lija lisanathe. Mwina mphunzitsi akhoza kunena kuti, "Ngati muli ndi mafunso, muloze dzanja lanu kumwamba. Tiima ndi kuyankha funso lanu." Mphunzitsi wabwino amanena miyambi kapena nkhani kuti ana aphunzire msanga ndi kumvetsetsa bwino.

6. KULOWEZA

Ichi ndi njira imodzi yakale ya kaphunzitsidwe. Pakugwiritsa ntchito njira imeneyi anyamata Achiyuda anaphunzira mabuku atatu oyamba a m'Buku Lopatulika. Anyamata oyamba amene anali kuphunzira Buku Lopatulika anaphunzira Chipangano Chakale chonse. Phunziro lililonse la Sande Sukulu lili ndi ndime ya pamtima. Muyenera kuiphunzitsa sabata iliyonse. Mpingo yambiri ili ndi njira yophunzirira Buku Lopatulika pa kuloweza mabuku a m'Buku Lopatulika ndi ndime zimene amasankha. Tiyenera kuwaphunzitsa achinyamata m'mene angaloweze pamtima Mawu a Mulungu. Izi ndi zina mwa zinthu zimene zingakuthandizeni:

- (a). Mugwiritse ntchito nyimbo.
- (b). Mugawe kalasi ija m'magulumagulu kuti athandizane.
- (c). Muyese kuwalimbikitsa kuti alembe ndime ya pamtima ija kokwanira makumi awiri ndi kasanu (25 taimusi).
- (d). Mudzichita mpikisano m'magulumo.
- (e). Mpingo uyenera kuzindikira anthu amene amaloweza pamtima ndime zokwana 52 pa chaka chimodzi.

7. KUKAMBIRANA PAMODZI

Anthu ayenera kukhala pamodzi monga gulu ndi kumakambirana za phunziro lija ndi kumafunsana mafunso ndi kumayankha. Mwachitsanzo: Mwina gulu likhoza kukambirana za m'mene Paulo anali kuyambitsira matchalitchi ndi udindo wathu ifenso kuyambitsa matchalitchi. Mphunzitsi, abusa ndi anthu ena awiri amene ali kudziwapo za kayambitsidwe kamatchalitchi akhoza kukhala pa gulu limeneli. Akhoza kukambirana njira zake m'mene angayambire matchalitchi atsopano.

8. MAGULU OMVETSERERA

Kalasi ija iyenera kugawidwa m'magulu awiri. Gulu lililonse liyenera kupatsidwa chinthu chakuti liphunzire. Pakutha pa phunziro lija gulu lililonse lifunsiwa kuti lifotokoze zimene laphunzira pa mutu umene linapatsidwalo. Mphunzitsi aphunzitsa; ana ndi kumamvetsera ndi kumafotokozaza zimene aphunzirazo. Mwachitsanzo: Mphunzitsi awerenge anthu amene ali pa kalasi yakeyo ndi kugawa kalasiyo m'magulu awiri. Gulu loyamba liwerenge malamulo khumi a Mulungu ndipo limvetsera Mawu amene akuti "usachite." Gulu lachiwiri limvetsera malamulo khumi amene ali ndi malonjezano. Gulu lililonse lifotokoza zimene lapeza.

9. KUSEWERA M'MALO MWA MUNTHU WINA

Munthu akhoza kutenga gawo la munthu wina pa masewero. Zikatha, gulu lija limakambirana zimene zachitika. Mwachitsanzo: Mphunzitsi ndi anyamata aja akhoza kuchitira umboni kwambiri ngati sewero limenelo litachitika bwino. Mnyamata m'modzi akhoza kutenga gawo la munthu woledzera, mkhristu amene sapita kutchalitchi ndipo ndi munthu amene ali kufuna kupeza Ambuye. Sewero litatha gulu lija limakhala pansu ndi kukambirana zimene zachitika ndikuona m'mene angachitire bwino nthawi zina.

10. UMBONI

Munthu amanena umboni wa zinthu zimene zinamuchitikira. Nthawi zambiri umboni umenewu umakhudzana ndi m'mene munthuyo anapulumutsidwira ndi pakupereka chakhumi. Nthawi zambiri imeneyi ndi njira yabwino. Anthu amakondwera akamva munthu wina ali kufotokoza m'mene anapulumutsidwira. Mwachitsanzo: Tiyeze kuti phunziro lanulo ndi la pemphero. Mphunzitsi akhoza kufunsa anthu awiri kapena atatu kuti afotokoze m'mene Mulungu anayankhira mapemphero awo.

Mphunzitsi akhoza kuthandizidwa ndi umboni wa anthu atatuwa pakuphunzitsa kapena pa nthawi imene magulu aja ali pamodzi ndi nthawi ya zokambirana.

6. BUNGWE

Werengani mutu 5, Kukulitsa Matchalitchi Kupyolera Sande Sukulu.

(1). Zaka - Pa gulu ili la Sande Sukulu ophunzirawo ayenera kukhala ndi zaka 13-20. Amenewa ngati ali ku Sukulu mwina akhoza kukhala kuti ali ku Secondary School.

Kalasi iliyonse idzikhala ndi anthu okwanira 20. Mukhoza kukhala ndi kalasi ya achinyamata, ochepa, ndi akulupo ndi ena amene akuoneka akuluakulu ndithu. Mpingo uli wonse udzikhala ndi makalasi molingana ndi anthu amene ali m'tchalitchimo.

(2). MALO - Pa mutu 5, Kukulitsa Tchalitchi Kupyolera Sande Sukulu muwerenga pegi 25-26. Apanso, mpingo uli wonse uyenera kusankha malo amene kalasi iliyonse idziphunzirira. Achinyamata akhoza kumaphunzirira m'nyumba ya abusa kapena kuseri kwa tchalitchi. Ndi chinthu chofunika kuti kalasi iliyonse ikhale ndi malo akeake ophunzirira sabata ndi sabata.

(3). NTHAWI - Mpingo uyenera kupanga nthawi yoyambira Sande Sukulu. Nthawi zambiri Sande Sukulu imayenera kuyambika mapemphero asanayambike. Nthawi yake iyenera kukhala mphindi 45-60. Mphunzitsi ayenera kukonzekera kuphunzitsa mphindi 45-60. Muyenera kuyamba nthawi yabwino kuti muthenso nthawi yabwino.

(4). MABUKU OPHUNZITSIRA - Maphunziro achinyamata a Sande Sukulu amapezeka ku I.P.S. Zimenezi zimakhala zokonzedwa kuti zithe zaka 5 ndipo zikhoza kugwiritsidwa ntchito ku magulu onse. Pakali pano tilibe mabuku aphunzitsi, tsono mphunzitsi ayenera kuti awerenge mabuku amenewa ndi mabuku a Sande Sukulu ndi achinyamata otchedwa Youth Division.

(5). KUSINTHA MAKALASI - Kuyamba kwa chaka chiri chonse mphunzitsi ayenera kusintha pa kalasi. Ana amene anali mu kalasi ya akachisi akhoza kukalowa kalasi ina yatsopano. Mukhoza kukonzekera nthawi yabwino ya kulandira anthu amene ali kulowa m'makalasi atsopanowa. Ngati muli ndi makalasi awiri achinyamata ena akalowa kalasi inayi pamene ena amene anali mukalasi ya achinyamata akuluakulupo akalowa kalasi ya akulu.

7. KUCHEZERA

Pali anyamata ambiri amene sapita kutchalitchi. Pa sabata amangoyendayenda kumapita ku misika, ndi kumayendayenda m'misewu. Sakondweretsedwa ndi kupita kutchalitchi, makamaka ku Sande Sukulu. Koma achinyamata amenewa afunika kuti adziwe Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo ndi Mfumu ya moyo wawo. Ndi ntchito ya Sande Sukulu kuwachitira umboni ndi kuwaphunzitsa.

Tsono, inu monga mphunzitsi wa Sande Sukulu umenewu ndi udindo wanu. Mudzilankhula nawo anyamata kuli konse kumene mwakumana nawo. Muyenera kuti mukhale bwenzi la anyamata, mudziyesera kuchita zimene ali kuchitazo. Muwaitane kuti abwere ku mapemphero a pakati pa sabata. Mukacheze nawo kunyumba kwawo. Akakhala ndi masewero ku sukulu kwawo mudzipita kukaonera masewerowo. Musaiwalenso ana amene amaliza sukulu; amenewa nthawi zambiri amakonda akuluakulu kuti adziwathandiza. Muone zimene amachita anyamata pa nthawi imene kuli ukwati kumudzi, maliro kapena ku msika. Muyese kucheza nawo; mumvetsetse zimene amalankhula. Muyesetse kumagwirizana nawo ndi kukhala nawo pa chibwenzi.

ZOPHUNZITSIRA APHUNZITSI SANDE
SUKULU YA AKULU

ZOPHUNZITSIRA APHUNZITSI SANDE SUKULU YA AKULU

Kodi munakhalapo ndi mtima wofuna kuti mpingo wanu ukule? Kodi mumadziwa kukoma kwake ngati munthu walandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wake ndi kuzindikira tanthauzo lake lenileni la moyo kupyolera kukula mumzimu? Zofuna zimenezi zili muntima wa Mulungu amene amatikonda ife tonse ndipo amafuna kutichitira zinthu zabwino. Yesu anati, "Koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha" (Yohane 4:14). Madzi a moyo amene Yesu Khristu ali kunenawo akhoza kupezeka mumpingo mwanu ngati mumpingo wanuwo uli ndi Sande Sukulu ya moyo ndi ya mphamvu.

CHOLINGA NDI NTCHITO YAKE YA SANDE SUKULU

Cholinga cha Sande Sukulu ndi kutumiza anthu a mumpingo kukachitira umboni kwa anthu amene sanadziwe Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wawo. Pa Sande Sukulu yabwino mamembala amayesetsa kubweretsa kwa Yesu anthu amene sanapulumsidwe. Timakwaniritsa lamulo lalikulu la Yesu Khristu, Mateyu 28:19-20, pamene tili ndi Sande Sukulu ya mphamvu.

Ntchito za Sande Sukulu ndi izi:-

1. KUCHEZERA - Kuchezera anthu ndi kuwapeza m'nyumba zawo, m'mizinda ndi kumidzi imene ili kutali ndi matauni. Tiyenera kumapita kumene kuli anthu.
2. KUPHUNZITSA- Kuwaphunzitsa Buku Lopatulika. Buku Lopatulika ndiye Buku lofunikira pa Sande Sukulu. Mawu a Mulungu ndi "Nyale ku mapazi anga ndi kuwala pa njira yanga" (Masalmo 119:11).
3. KUWABWERETSA - Kuwabweretsa kwa Yesu Khristu. Taona kuti nthawi zambiri anthu akhoza kulandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wawo pamene awerenga Buku Lopatulika kawirikawiri ndi akhristu. Tiyenera kumakhala ndi anthu amene sanapulumsidwe pa Sande Sukulu ndi cholinga chakuti tiwabweretse kwa Yesu Khristu.
4. KUTUKULA - Tiyenera kuwatukula ndithu mpaka titaona kuti akhwima. Pa Sande Sukulu paga akamaphunzira Mawu a Mulungu ndi kukhala ndi chiyanjano pamodzi, adzakula pamodzi m'chikhulupiro ndi kukula m'Chikhristu chawo. Buku Lopatulika limatiuza kuti tiyenera kukhala anthu "oyera." Zimenezi zimatanthauza

kuti pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, nzeru zathu, chikondi ndi mphamvu ziyenera kumakula kupyolera mwa Mzimu Woyera.

5. KUTUMIKIRA - Kutumikira zosowa za anthu. Ife pakuti ndife akhristu, timathandiza anthu m'dzina la Yesu Khristu. Makalasi a Sande Sukulu onse amagwira ntchito pamodzi ndipo kalasi iliyonse pa yokha imachita chifuniro cha Mulungu kuthandiza anthu amene ali osowa kuphatikiza amene amapemphera pamodzi ndi amene sapemphera.

BUNGWE

Sande Sukulu iyenera kulongosoka bwino kuti ntchito igwiridwe bwino. Tsono antchito ayenera kuphunzitsa ndipo aliyense ayenera kupatsidwa ntchito kuti adzichita kuti cholinga ndi ntchito yake ya Sande Sukulu ikwaniritsidwe. Sande Sukulu imafunika kukhala ndi atsogoleri amphamvu: abusa, atsogoleri ampingo, ndi madikoni. Mtsogoleri, mlembi ndi aphunzitsi ayenera kusankhidwa ndi kuphunzitsidwa m'mene angatsogolere Sande Sukulu.

Pakuti Sande Sukulu ndi ya munthu aliyense, payenera kukhala dongosolo loika anthu m'magulumagulu molingana ndi zaka zawo pakuphunzira Mawu a Mulungu. Ana, achinyamata ndi akulu amamva zinthu mosiyana, tsono ayenera kugawidwa m'magulu molingana ndi zaka zawo. Sangogawidwa m'magulu amenewa chifukwa cha kuphunzira kokha, komanso chifukwa cha chiyanjano, chimenenso chili chinthu chofunika pakukula m'Chikhristu chathu.

Sande Sukulu iyenera kukhala ndi magulu awa:

Ana Akachisi	zaka 4-6
Ana Akulupo	zaka 7-12
Achinyamata	zaka 13-20
Akulu	zaka 21 kupita mtsogolo

Magulu amenewa akhoza kusinthika, malingana ndi kufuna kwanu, komabe anthu amaphunzira bwino akakhala m'magulu. Munthu akakwatira, amamuganizira kuti ndi munthu wamkulu, ndipo tsopano ayenera kukhala m'gulu la amene anakwatira.

GULU LA AKULU

Kodi chifukwa chiyani timaphunzitsa anthu akulu? Kodi Sande Sukulu, si ya ana okha? Mudzamva makangano amenewa nthawi zambiri. Kodi chifukwa chiyani akulu amapitirira

kuphunzira Sande Sukulu? Kodi sikwabwino kuti akulunso azipita ku mpingo pa tsiku la sabata ndi kuphunzira Mawu a Mulungu? Pamene tili ndi moyo timafunika kuphunzira Buku Lopatulika. Ngati timadziwa kwambiri Buku Lopatulika, ndi bwino kuti tikhale pa Sande Sukulu kumathandiza anzathu. Koma ambiri mwa ife, tili kuphunzira kumene. Indedi, Sande Sukulu ndi ya munthu aliyense pamodzi ndi akulu omwe. Aphunzitsi a Sande Sukulu ya akulu ayenera kuyesetsa kuti anthu ali kuthandizidwa ndi maphunzirowo.

Kodi chifukwa chiyani akulu ayenera kuphunzira Mawu a Mulungu? Umoyo wa akulu ufunikadi kudalira pa Buku Lopatulika ndi maphunziro ake. Akulu a zaka zokwana makumi awiri mpaka atatu amaganizira zinthu zazikulu monga ukwati, ntchito kapena kumene adzakhala, maphunziro ndi ana amene adzabadwa m'banja lawolo. Akulu a zaka makumi anayi mpaka makumi asanu ndi limodzi akupsyinjika ndi ntchito ya banja, ntchito yawo, ndalama zolipira sukulu ndi zothandizira pa banja pawo ndi achibale awo. Kutichite zimenezo, ayenera kukhala ndi mphamvu za Mulungu wa moyo.

Akulu okwana zaka makumi asanu ndi limodzi mpaka ukalamba wawo akuganizira za ukalamba wawo ndi kukhala pa okha chifukwa cha umasiye, ana ali kukwatira ndi kukwatiwa ndi za kupeza chiongola dzanja chawo cha pa ntchito.

Akulu amaphunzira bwino pamodzi ndi iwo amene ali ofanana nawo zaka, abambo kapena amayi. Amaphunzira bwino ngati mphunzitsi ali kuwakonda ndi kuonetsa chidwi pa moyo wawo wa Chikristu. Mphunzitsi wa Sande Sukulu ayenera kukhala bwenzi lenileni la Chikristu, mlangizi ndi mtsoholeri.

Akulu amaphunzira bwino ngati auzidwa kuti awerenge Mawu a Mulungu pa okha, m'kalasi momwemo ndi nthawi zina. Amaphunzira ngati atsogoleredwa kuti awerenge pa gulupo. Akulu amaphunzira bwino koposa pamene apatsidwa mwayi wakuti achite kanthu ndi zinthu zimene apatsidwa. Nthawi zina zochita zawo zikhoza kuwathandiza kuti azindikire kuti ayenera kusintha mtima. Akaphunzira bwino, miyoyo yawo imasintha kupyolera mwa Mzimu Woyera wa Mulungu.

MPHUNZITSI WA AKULU

Pamene Mulungu anakuitanani kuti mukhale mphunzitsi wa akulu, anakulemekezani kwakukulu ndiponso anakupatsani udindo waukulu. Tiyeni tilembe zinthu zofunikira kuti munthu akhale mphunzitsi wa akulu.

1. Abambo ndi amayi ayenera kukhala mkhristu amene anabadwanso. Mphunzitsi ayenera kukhala ndi umboni wa chikhulupiriro chake mwa Yesu Khristu chifukwa zimenezi zidzakhala gawo lalikulu pa utumiki wake pa kalasi yake ija. Simungathe kuuza anthu ena zinthu zimene inu simunazione kapena kuzichita. Mpingo uyenera kuona kuti aphunzitsi onse ndi akhristu.
2. Abambo ndi amayi ayenera kukhala mkhristu amene anabatizidwa ndiponso amene amathandiza mpingo wake. A Baptist amakhulupira mpingo monga kumene kumayambira ntchito ya Chikhristu, tsono mphunzitsi ayenera kupereka chitsanzo kumpingo kwakeko.
3. Abambo ndi amayi ayenera kukhala munthu amene amakonda kuwerenga Buku Lopatulika. Pakuti Buku Lopatulika ndilo buku limene limagwiritsidwa ntchito pa Sande Sukulu, munthu amene amamvetsa bwino Buku Lopatulika ndi ziphunzitsi za Baptist. Tiyezi tigwiritse ntchito 1 Timoteo 3:6, "Asakhale wophunza, kuti podzitukumula umgangwere mlandu wa mdierekezi."
4. Bambo ndi Amayi ayenera kukhala munthu amene amafuna kuphunzira. Ntchito yophunzitsa imafunika munthu amene amafuna kudzitukula yekha ndipo akatero amakhala mphunzitsi wamphamvu.
5. Mphunzitsi ayenera kumachezera anthu, kumawachitira umboni ndi kubweretsa anthu kwa Yesu.
6. Mphunzitsi ayenera kumapereka chitsanzo pa kupereka chakhumi. Buku Lopatulika limanena poyera pa za udindo ndipo kalasi imene tili kuiphunzitsayo imatsatira zimene ife tili kuchita monga aphunzitsi.

1. KUKONZEKERA PHUNZIRO

Poyamba tisanaone m'mene mphunzitsi angakonzekere, tiyenera kudziwa kuti ayamba liti? Tsiku la sabata, madzulo ndi nthawi yabwino yokonzekera phunziro la sabata ya m'mawa. Pakuphunzira phunzirolo mphindi 30 tsiku ndi tsiku, mphunzitsi adzaloweza bwino phunzirolo. Iye adzakonzeka tsopano kuphunzitsa pa sabata. Ngati munthu ayamba mochedwa kuphunzira phunzirolo monga usiku wa tsiku la chiweru kapena kudikira mpaka pa tsiku la sabata, sangapeze nthawi yokonzekera bwino kuti akaphunzitse bwino. Phunzirani zina tsiku ndi tsiku.

1. Muyambe ndi pemphero. Mufunse Mulungu kuti atsogolere maganizo anu ndi ntchito imene mudzaichita paphunziro lanulo. "Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha kudziwa" (Miyambo I:7).
 2. Muphunzi ndime ija kuchokera m'Buku Lopatulika pa nokha popanda munthu wina wokuthandizani. Mulembe zimene Mzimu Woyera wakuuzani.
 3. Tsopano muwerenge mabuku ena amene angathenso kukuthandizani monga buku la aphunzitsi ndi buku la ana limene muli maphunziro ophunzitsira, monga mabuku ena amene mungakhale nawo monga makomentare, dikishonale ndi konkodansi. Tsopano mulembe zimene mwazona ndi zinthu zimene mwazimva kuchokera ku mabuku enawo. Zimenezi zikuthandizani pakuphunzitsa.
 4. China, mutsirize kulemba gawo la pamwamba paphunzirolo (Mwachitsanzo).
2. KUKONZEKERA ZIMENE MPHUNZITSI ANAPANGA
- (a). Tsiku _____ Mutu wa phunziro _____
Ndime _____
 - (b). Choonadi chenicheni _____

 - (c). Kodi phunziro ili lingawathandize bwanji anthu a makalasi? _____

 - (d). Cholinga cha phunziro _____

 - (e). Kodi ndili kufuna kuti kalasi yanga ichite chiyani pakutha paphunziro ili? _____

- a. Mulembe tsiku, mutu wa phunziro ndi ndime ya m'Buku Lopatulika. Muganizire chimene muli kufuna kuti anthu adziwe ndi kufanizira ndi phunziro la sabata ino, zimenezo zingafanane ndi zimene muli kufuna kuti anthu adziwe.
 - b. Mulembe choonadi cha phunzirolo. Muyenera kulemba monga m'mene muli kudziwira.

- c. Mulembe zosowa za anthu amene muli kuwaphunzitsawo ndipo ndi m'mene phunziro limeneli lingathandizire zosowa za anthuwo.
- d. Mulembe cholinga cha phunziroli. Cholinga chabwino chimayenera kukhala chomveka bwino kuti anthu adzikumbukira bwino.
- e. Kodi muli kufuna kuti anthu aja aphunzire chiyani, kapena muli kufuna kuti asinthe makhalidwe awo kapena muli kufuna kuti achitepo kanthu? Mukhale ndi chinthu chimene muli kufuna kuti achite pakutha paphunziroli.
5. Kukonzekera zimene zidzachitika m'kalasi. Mulembe m'mene mudzidzaphunzitsira. Mudzifunse nokha mafunso. Kodi ndidzichita chiyani m'kalasimo? Kodi ndiwatsogolere bwanji anthu amene ndili kuwaphunzitsawa kuti nawo adzitenga gawo lawo pamene ali kuphunzira?

3. KUKONZEKERA ZA M'KALASI

- (a). Ndidzayesetsa kuti anthu aja akhale ndi chidwi pakuchita izi _____
- (b). Ndidzathandiza kalasi yanga kutenga zimene ndili kuwaphunzitsa kuti zikhale gawo limodzi la moyo wawo pakuchita izi _____
- (c). Ndidzathandiza kalasi yanga kukhala ndi chidwi pakuphunzira Buku Lopatulika pakuchita izi _____
- (d). Ndidzalimbikitsanso anthu kuti apitirize kuphunzira Buku Lopatulika pakuchita izi _____

Pali zigawo zinayi pa dongosolo la kuphunzitsa.

- (a). KUKHALA NDI CHIDWI CHA OPHUNZIRA KAPENA KUTI OPHUNZIRA AYENERA KUMAZIKONDA ZIMENE ALI KUPHUNZIRA ZIJA

Ndime iyi iyenera kuthandiza ophunzira kuti aganizire pamodzi za mutu wa phunziroli. Mphunzitsi ayenera kuyamba

ndi zinthu zimene ophunzira amazidziwa kale. Pa Yohane 4, Yesu pa chitsime paja, anapempha mayi uja kuti amupatse madzi. Zimenezi zinamuthandiza kuti amuuze za madzi a moyo. Iyi ndiyo njira yofunika pakuphunzitsa. Mawu oyambira ayenera kufanana ndi phunziro. Mawu ena ayenera kukonzedwa bwino kuti akhale ngati "ulalo" pakati pa mawu oyambira ndi kuphunzira Buku Lopatulika lenileni limene lidzaphunzitsidwa. Mwachitsanzo, Yesu anati, "Ukadadziwa mtulo wa Mulungu, ndi Iye amene alinkunena ndi iwe, undipatse Ine ndimwe, ukadapempha Iye, ndipo akadakupatsa madzi a moyo" (Yohane 4:10). Musaiwale kukonzekera "mlatho."

b. ANTHU PA KALASI PAJA AYENERA KUMAPHUNZIRA BUKU LOPATULIKA

Limeneli ndi gawo lofunika paphunziro. Mwaphunzira ndime za m'Buku Lopatulika, ndipo muli kudziwa zimene mukaphunzitse. Tsopano funso ndi lakuti, kodi mukonzekera bwanji kuti zimenezi zithandize kalasi yanuyo?

Kodi ndimezo zidzawerengedwa bwanji? Pamaso pa kalasi yonse munthu m'modzi adzaimirira ndi kuyamba kuwerenga. Mphunzitsi akhoza kuwerenga ndime yonse. Sibwino kufunsa munthu amene sadziwa kuwerenga kuti awerenge, mwina tikhoza kumuchititsa manyazi.

Kodi, tsopano ndi chiyani chimene mwakonzekera kuti kalasi yanu idzichita? Kodi adzingomvetsera? Kodi muli kukonzekera kuti adzikafunsa mafunso kapena adzikayankha mafunso? Mulembe chikonzero chanu pa gawo ili.

c. KUGWIRITSA NTCHITO ZIMENE TAPHUNZIRA PA MOYO WATHU

Ngati kuphunzitsa kumangochokera m'mutu kapena m'nzeru za munthu, kumeneko sikuphunzitsa kwabwino. Nzeru pa zokha sizingathe kuchita kanthu ngati sizibala chipatso. Ngati palibe kusintha pakati pa anthu m'machitidwe kapena nkuganiza ndiye anthuwo sali kuphunzira.

Yesu anamuuza mabvuto ake a mayi uja pa chitsime paja. Tili kukhala m'dziko la mabvuto. Mphunzitsi ayenera kuphunzitsa ndime zimene zikhoza kuthandiza anthu kuti asinthe makhalidwe awo. Ngati mphunzitsi akutsogolera anthu kudzipereka pa miyoyo yawo, ali kuphunzitsa bwino. Mphunzitsi ayenera kukonzekera zimenezi kuti anthu adzipereka.

d. KULIMBIKITSA ANTHU KUTI APITIRIZE KUWERENGA BUKU
LOPATULIKA

Konzekerani kuti kalasi yanu ilimbikitsidwe kuphunzira Mawu a Mulungu. Musankhe ndime yakuti muwerenge ndi kuwalimbikitsa kuti adziwerenga pakati pa sabata. Mphunzitsi akhoza kubweretsa ndime zina za m'Buku Lopatulika kuti kalasi yakeyo ipitirize kuwerenga. Werengani gawogawo. Njira zabwino zophunzitsira Sande Sukulu, mu Bukuli kuti mupeze zimene mungachite pa magawo anayi a bungwe la kuphunzitsa.

DONGOSOLO LA SANDE SUKULU

Maphunziro a Sande Sukulu amakonzedwa m'magulumagulu. Zimenezi zimachitika choncho kuti mitu yosiyanasiyana ya m'Buku Lopatulika zingaphunzitsidwe. Magulu ena anangolembedwa m'ndime zokhazokha, enanso mitu yokha ya m'Buku Lopatulika kuti tiziphunzira. Njira zonsezi ndi zabwino ndipo zonsezi zili ndi thandizo lake.

Nyumba ya Baptist imene imasindikiza mabuku ikhoza kukuthandizani kwambiri kuti mupeze mabuku. Tiyeni tionetsetse kuti tili ndi mabuku abwino amene akhoza kutithandiza. Mipingo ina imakhala ndi mabuku ndi mapepala ena amene amapatsa anthu kuti adziwerenga, koma tiyenera kuchenjera, mwina zimenezo zikhoza kutisokoneza.

Muthandize mpingo wanu pakugula ndi kugawa ndi kugwiritsa ntchito mabuku a Baptist. Zinthu zimenezi timazikonza nthawi ndi nthawi. Muyenera kudziwa kuti timachita zimenezi kufuna kuti tikuthandizeni kuwerenga ndi kuphunzira Buku Lopatulika limene lili buku la Sande Sukulu.

KUCHEZERA

Mphunzitsi wina amene anali Evangelist analemba buku lakuti, "Pamodzi ndi Khristu kukafunafuna otayika." Chimenechi ndi cholinga chabwino cha Sande Sukulu. Yesu ananena mwambi nati, "Ndipo Mbuye ananena kwa kapoloyo, Turuka, nupite kumisewu ndi njira za kuminda, mwaumirize anthu alowe, kuti nyumba idzale" (Luka 14:23). Munthu wina anati, "Sangobwera, tiyenera kukawatenga; sangaphunzire, ayenera kuphunzitsidwa." Sande Sukulu iyenera kumachezera anthu kuti adzibwera ku mpingo. Pa Sande Sukulu paja muyenera kulemba maina a anthu amene munakachezerawo, tsono ndi kugawa anthu m'magulumagulu kuti agwire ntchito imeneyi ndipo Sande Sukulu ikhoza kuchita ntchito imeneyi kuposa gulu lina lililonse. Ntchito yaikulu imapepuka ngati mwagawa anthu m'magulumagulu kuti aichite.

Pamene aphunzitsi kapena atsogoleri a Sande Sukulu atsogolera kukachezera anthu, mpingo ukhoza kukhala ndi anthu ambiri posachedwa.

Nthawi zonse tidzikhala ndi nthawi yoyambira kukachezera anthu ndi kukhala ndi nthawi yopemphera pamodzi musanayambe ntchito yanuyo. Mubwereko nthawi yabwino kuti mudzauzane zimene munakazona ndi kutseka ndi pemphero. Imeneyi ndi ntchito yofunika kwambiri pa mpingo.

MNDANDANDA WA PA SABATA M'MAWA

Chinthu china chokondweretsa cha Sande Sukulu ndi chakuti anthu amakumana pa sabata lililonse ndipo pa nthawi yabwino ndi m'mawa mapemphero asanayambike. Imeneyi ndiyo nthawi yabwino imene mipingo yambiri imalola kuti Sande Sukulu idzichitika pa ola limodzi, pamene mapemphero asanayambike. Sande Sukulu iyenera kuyambika pa 9:30 pamene anthu onse akumana pamodzi kuimba nyimbo, mapemphero, zolengeza ndi kuwerenga ndime ya m'Buku Lopatulika. Muyenera kumasamalira nthawi, osapitiriza pa mphindi khumi ndi zisanu. 9:45 kupita ku makalasi ndi kuyamba kuphunzitsa. 10:25 kutsiriza kuphunzitsa. 10:30 nthawi ya mapemphero. Zimenezi zimasintha malinga ndi m'mene mpingo ungafunire, koma chofunika ndi kuti Sande Sukulu ija iyenera kukhala ndi nthawi yokwana. Ngati aphunzitsi aja ndi ophunzitsidwa bwino, okonzeka ndi odzipereka, adzafuna kuti akhale ndi nthawi yambiri yophunzitsira. Phunziro likhoza kutenga nthawi yaitali ngati mphunzitsi alola kuti kalasi yakeyo idzitenganso gawo. Sibwino kumachita zinthu mothamanga. Mudziwapatsa nthawi kuti adzimvetsetsa zimene muli kuphunzitsazo.

Muwatsogolere anthu kuti afikira pa nthawi yabwino. Akhoza kumafika nthawi yabwino ngati lamulo lakuti adzifika mofulumira ndipo akatero muwapatse zochita. Muyambe mofulumira kuti mutsirize nthawi yabwino.

NJIRA ZINA ZABWINO ZOPHUNZITSIRA

Yesu ndi Mphunzitsi wamkulu amene anali kuphunzitsanso Uthenga wamphamvu. Njira zakenso zinalinso zabwino. Anali kuuza anthu miyambi. Anali kuwafunsa mafunso ndiponso anali kuyankha mafunso amene anali kumufunsa anthu aja. Anali kugwiritsa ntchito zinthu zimene anthu amazidziwa kale. Izi ndi njira zina zophunzitsira zimene mukhoza kuzigwiritsa ntchito.

1. KUPATSA KALASI CHIDWI

- (a). Fanizo - Kugwiritsa ntchito chinthu chimene chili chozolowereka. Yesu anagwiritsa ntchito madzi kupatsa mkazi uja chidwi.
- (b). Kubwereza mawu. Werengani mawu ochokera m'Buku Lopatulika, nyuzi pepala, kwa munthu wodziwika kapena mwambi wodziwika bwino.
- (c). Chiwerengero - Mwina chiwerengero cha anthu cha mumpingo chimasonyeza chiwerengero choonadi, kutukuka, chenjezo kapena chilimbikitso.
- (d). Ndakatulo zimathandiza ngati zili ndi tanthauzo.
- (e). Zinthu zatsopano - Nkhani za m'dziko lapansi ndi m'dera lathu ndi fanizo labwino pa zosowa zathu zingathandize chidwi pa kalasi.
- (f). Mafunso okonzedwa kale amathandiza kalasi. Adzathandizanso mphunzitsi kuona zofunika za kalasi yake.
- (g). Mbiri ya munthu wina. Kuphunzira za munthu wina ndi kuona zimene zinachitika pa moyo wake zikhoza kupatsa chidwi kalasi, koma musapereke chitsanzo cha munthu amene ali mkalasimo. Funsani kuti, "Kodi mukadachita bwanji ngati _____?"
- (h). Makolasi amathandiza kalasi kuti itsitsimuke.
- (i). Masewero - Anthu ena m'kalasimo achite sewero kuti ena aonelere sewerolo. Zimenezo zimawathandiza kuti aone ndi kuphunzira bwino.

2. KUTHANDIZA KALASI KUTI IPITIRIRE KUPHUNZIRA BUKU LOPATULIKA

- (a). Kuphunzitsa - Mphunzitsi wabwino ayenera kumakonzekera bwino. Mphunzitsi ayenera kumaphunzitsa kuti anthu aja adzikumbukira ndi kusunga zimene waphunzitsazo.
- (b). Kufufuza - Ndime za m'Buku Lopatulika- anthu pa kalasi akamawerenga Buku Lopatulika amakhala ndi zinthu kapena ndime imene ali kufuna. Zimenezi zikhoza kuchitika pamene tili m'magulu ang'onoang'ono kapena pa nthawi yofunsa mafunso.

- (c). Mapu - Mulembe mapu pa bolodi kapena pansi ndi ndodo. Kumbuyo kwa Buku Lopatulika lanu kuli mapu. Anthu adzakumbukira zinthu zimene amazona.
- (d). Ripoti - Anthu muwapatse zinthu zolembalemba kale kuti awerenge m'kalasi momwemo.
- (e). Magulu ang'onoang'ono - Mugawe kalasi yanu m'magulumagulu ang'onoang'ono kuti ayankhe mafunso kapena akambirane zimene aphunzira.
- (f). Kulemba pa pepala phunziro lanu ndi m'mene mukaphunzitsire. Zimathandiza pophunzitsa zimenezi. Mukhoza kulemba pa bolodi, papepala, kapena pansi.
- (g). Mafunso/ndi kukambirana - Mufunse mafunso ndi kulola kuti kalasi ikambirane ndi kuthandizana kuyankha mafunso. Mphunzitsi ayenera kutsogolera pa zokambiranazo kuti aone kuti potsiriza cholinga chake chakwaniritsidwa. Ayenera kusamala kuti mafunsowo akhale ochokera paphunziro limene ali kuphunzitsalo.

3. ZIMENE MULI KUPHUNZITSAZO ZIYENERA KULOWA M'MOYO MWANU

- (a). Zinthu zimene timazona pa moyo wathu - Mufunse kuti, "Kodi mukadachita chiyani ngati _____?" Pa zinthu zooneka kapena zoganzira pa moyo wa munthu. Kalasi iyenera kukumbukira zimene zinalembedwa.
- (b). Kuthetsa mabvuto - Mugwiritse ntchito bvuto limene lili lodziwika ndi lokhudza phunzirolo. Muone zimene Mawu a Mulungu anena.
- (c). Kupemphera - Kalasi idzikhala ndi nthawi ya mapemphero.
- (d). Umboni - Mulembe umboni umene anthu amaupeza pa moyo wawo ndipo mupatse aliyense m'kalasimo. Muwafunse kuti afotokoze m'mene Mulungu wathandizira pa moyo wawo.

4. KULIMBIKITSA ANTHU KUTI APITIRIZE KUPHUNZIRA BUKU
LOPATULIKA

- (a). Zinthu zochita - Mufunse kalasi yanu kuti awerenge Buku Lopatulika ndi kudza fotokozera ku kalasi yonse sabata yamawa.
- (b). Zinthu zoloweza pamtima - Kuloweza ndime za m'Buku Lopatulika kumathandiza munthu kuti adzikumbukira Mawu a Mulungu. Muyenera kuwapatsa ndime zofunikira.
- (c). Mafunso - Mulembe mafunso ndipo muwapatse potsiriza paphunzirolo. Mafunso amenewa adzayankhidwa sabata yamawa ndipo ayenera kubwera okonzekeratu.
- (d). Mabvuto - Mulembe mabvuto amene munthu amawapeza pa moyo wake ndi kupatsa munthu aliyense m'kalasimo. Muwafunse kuti alembe m'mene angachitire mothandizidwa ndi Buku Lopatulika.

Pali njira zochepa zimene zingagwiritsidwe ntchito. Mukhoza kusankha sabata iliyonse zimene mukhoza kugwiritsa ntchito. Pakuwerenga, kukonzekeratu komanso ophunzira aja ayenera kumachita gawo lawo, mukatero zinthu zimene muli kuphunzitsazo zidzagwira ntchito m'miyoyo ya anthu aja.

POTSIRIZA

Musaiwale kuti Ambuye Yesu Khristu anali mphunzitsi wa akulu. Nthawi zambiri anthu anali kumutcha mphunzitsi (Rabbi). Akulu ali kudikira munthu wina ngati inu amene ali ndi Uthenga wochokera m'Buku Lopatulika. Amasowa chiyanjano cha mumpingo chimene Sande Sukulu ikhoza kubweretsa m'miyoyo yawo. Inuyo, ntchito yanu, monga mphunzitsi wa Sande Sukulu ya akulu mufunika kuchita ntchito ya mphamvu, koma ndi ntchito ya bwino ndi yopindulitsa.

KUKONZEKERA KWA MPHUNZITSI

1. Kukonzekera zapamtima panu.
 - (a). Pemphero.
 - (b). Kuwerenga Buku Lopatulika.
 - (c). Kuwerenga buku la aphunzitsi.

2. Kukonzekera cholinga cha phunziro.
 - (a). Tsiku _____ Mutu wa Phunziro _____ Mawu a Mulungu
 - (b). Choonadi chenicheni _____
 - (c). Kodi phunziro ili lili kugwilizana bwanji ndi anthu a m'kalasi mwanga muja? _____

 - (d). Cholinga cha phunziro _____

3. Kukonzekera za m'kalasi.
 - (a). Ndidzayesetsa kuti kalasi yanga idzikonda maphunzirowa pakuchita izi _____

 - (b). Ndidzakopa kalasi yanga kuti adziphunzira ndi kuwerenga Mawu a Mulungu pa okha pakuchita izi _____
 - (c). Ndidzathandiza kalasi yanga kuika zimene ndinawaphunzitsa m'miyoyo yawo pakuchita izi _____
 - (d). Ndidzalimbikitsa anthu kuphunzira ndi kuwerenga Mawu a Mulungu pakuchita izi _____

**KUCHITIRA UMBONI KWA ANTHU AMENE
SANALANDIRE YESU KHRISTU KUPYOLERA
M,SANDE SUKULU**

(Wolembe ndi Bambo Ross Collier)

**KUCHITIRA UMBONI KWA ANTHU AMENE SANALANDIRE
YESU KHRISTU KUPYOLERA M,SANDE SUKULU
(Wolembe ndi Bambo Ross Collier)**

Funso limene abusa ambiri amafunsa ndi lakuti, Kodi tchalitchi yanga ingakule bwanji? Mbusa aliyenso amafuna kuti tchalitchi yake idzikula. Tiyezi tione njira imodzi imene tchalitchi yathu ingakulire. Ndi njira imodzi imene yathandiza anthu ambiri dziko lonse lapansi pano. Njira imeneyi sigwira ntchito ku matchalitchi ang'ono okha kapena akulu okha ayi. Njira imeneyi yakhala ikuthandiza matchalitchi amitundu yonse kukula ndi mphamvu. Njira imeneyi idzakuthandizani m'mene mungapezere anthu amene sadziwa Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo, m'mene mungathandizire akhristu anu kuti adzikula m'Chikhristu chawo, m'mene tchalitchi yanu ingakulire ndi m'mene akhristu atsopano angakulire.

Njira imeneyi ndi Sande Sukulu. Sande Sukulu ndi bungwe limene lili lokonzeka kugwira ntchito yochitira umboni. Zifukwa izi zimapangitsa kuti Sande Sukulu ikhale chida cha mphamvu chokulitsira tchalitchi.

1. Sande Sukulu ilipo kale m'matchalitchi ambiri, tsopano palibe chifukwa chakuti tikhale ndi gulu linanso.
2. Ndi magulu a anthu okwanira 10-12, Sande Sukulu ikhoza kugwira ntchito yake bwino kuposana ndi gulu lina lililonse. Mphunzitsi wa Sande Sukulu ayenera kuti adzidziwana nawo bwino anthu amene ali kuwaphunzitsa aja.
3. Anthu amene ali kuphunzira Sande Sukulu aja akhoza kuchitira umboni bwino kwa anthu amene ali ofanana nawo misinkhu kuposana ndi anthu ena, mwachitsanzo, anyamata akhoza kuchitira umboni bwino anyamata anzawo ndiponso akuluakulu akhoza kuchitira umboni bwino akuluakulu anzawo.
4. Anthu amene asanalandire Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo akhoza kuyamba kuphunzira Sande Sukulu ngakhale asanalandire Ambuye kukhala monga Mpulumutsi wawo ndi Mfumu ya moyo wawo.
5. Ngati munthu amene asanalandire Ambuye monga Mpulumutsi wake ayamba nawo Sande Sukulu, amayamba kuganizira kuti ali gawo limodzi la mpingo ndipo amamvetsetsa bwino Uthenga Wabwino. Amakhala ndi chilakolako chakufuna kuphunzira za Yesu Khristu.

6. Gulu la Sande Sukulu pa kalasi iliyonse ngati pali anthu ochepa akhoza kumathandizana bwino ndi kumalimbikitsana pa chikhulupiriro chawo ndi kudziwanso msanga anthu amene sanalandire Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo. Akakumana kwina kapena kunyumba amakhala omasuka kuthandizana ndi kumachitirana umboni.
7. Sande Sukulu imachotsa maganizo amene anthu ambiri amakhala nawo akuti kuchitira umboni ndi ntchito ya abusa okha. Mkhristu aliyense ayenera kumachitira umboni.
8. Ntchito yakukulitsa tchalitchi imagawika m'magulumagulu. Mwachitsanzo, kalasi ya anthu 12 ikhoza kupangana kuti mwezi uli wonse pa gulu lawo adzichitira umboni kuti munthu m'modzi ayambe Sande Sukulu. Akatero ndiye kuti pakutha kwa chaka, Sande Sukulu yawoyo idzakhala ndi anthu a chilendo okwanira 12. Taganizirani ngati magulu onse a Sande Sukulu atakhala ndi cholinga chomwecho?
9. Ngati kalasi ija ikhala ndi anthu okwanira 20, ayenera kuti agawe kuti akhale makalasi awiri ndi kusankha mphunzitsi watsopano kuti adziphunzitsa kalasi yatsopanoyi. Izinso zimathandiza kuti tchalitchi ikhale ndi atsogoleri a mphamvu. Ngati Sande Sukulu ikula ndiye kuti mudzakhala ndi aphunzitsi ambirinso.
10. Ngati anthu amene asanalandire Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo abwera kudzapemphera nawo, timayembekeza kuti Mulungu akhoza kulankhula nawo kuti alandire Ambuye Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo ndi Ambuye wa moyo wawo. Sande Sukulu ndi malo amene anthu akhoza kukhala omasuka.

Zifukwa khumi zimenezi zimatithandiza ife kuti tiyankhe funso ili lakuti, "Kodi tchalitchi yanga ingakule bwanji?" Tchalitchi iyenera kuzindikira kuti Sande Sukulu ndi dongosolo limene lili ndi udindo wofalitsa Uthenga Wabwino kwa anthu ndipo tchalitchi iyenera kuzindikira mfundo izi kuti ithandize Sande Sukulu kuti ikule.

Poyamba, tchalitchi iyenera kuzindikira kuti ndi chikonzero chake cha Mulungu kuti tchalitchi ikule. Tchalitchi iyenera kulandira udindo wochitira umboni kwa anthu otaika, kuwaphunzitsa Buku Lopatulika ndi kuonetsa anthu kufunika kwake kwa kutumikira Ambuye.

Kachiwiri, mbusa ayenera kuti atsogolere tchalitchi yake kuti idzimvetsetsa Buku Lopatulika kuwaphunzitsa kuchitira umboni. Iye ndi mbusa wa tchalitchiyo. Ngati mbusa satsogolera tchalitchi yake kuti ithandize dongosolo

lakuchitira umboni, Sande Sukulu, sidzagwira ntchito yake bwino.

Mbusa ayenera kusonkhanitsa aphunzitsi onse a Sande Sukulu pamodzi ndi kukambirana zinthu izi:

1. Munthu ayenera kusonkhanitsa aphunzitsi onse a Sande Sukulu. Chiyenera kuchokera pansi pantima wake.
2. Sande Sukulu iyenera kukhala ndi anthu okwanira 20; kuti mphunzitsi awaphunzitse bwino, awatsogolere bwino. achite bwino utumiki wakewo ndipo kalasi yakeyo imakhala yomasuka ndiponso mphunzitsiyo amaphunzitsa ndi mphamvu.
3. Tchalitchi iyenera kusankha aphunzitsi amene ndi anthu okonda kuchitira umboni ndipo ndi anthu ofuna kuidziwa kwambiri ntchito yawoyo.
4. Kalasi ya Sande Sukulu iyenera kupanga dongosolo lochezera anthu sabata ndi sabata.
5. Sande Sukulu iliyonse iyenera kulemba dzina la munthu aliyense amene ali pa kalasipo.
6. Makalasi a Sande Sukulu onse ayenera kulemba anthu ambiri ngati kuli kotheka. Kalasi iliyonse iyenera kumalemba munthu m'modzi pa mwezi ngati kuli kotheka.
7. Sande Sukulu iyenera kumasunga maina a anthu ocheza ndi midzi yawo.
8. Sande Sukulu iliyonse iyenera kumachezera alendo onse amene abwera kudzacheza sabata kapena mwezi umenewo.
9. Ndi ntchito ya Sande Sukulu kucheza anthu onse amene sanabwera kutchalitchi sabata kapena mwezi umenewo.
10. Sande Sukulu iyenera kusunga maina a anthu amene amabwerabwera ku Sande Sukulu.
11. Ngati wina pa kalasipo sali kumvetsetsa, anzake ayenera kumuthandiza kuti amvetsetse bwino.
12. Mphunzitsi ayenera kufotokoza bwino kuti munthu aliyense akhoza kuyamba Sande Sukulu. Palibe kanthu ndiponso palibe kusiya ngakhale ndi mkhristu, kapena munthu wosapulumsidwa akhoza kuyamba Sande Sukulu.

13. Mphunzitsi ayenera kumalimbikitsa anthu aja kuti adzibwera ku Sande Sukulu msanga, kuti anthu aja akhoza kumaphunzirira pamodzi zinthu zonse.
14. Mphunzitsi ayenera kumalimbikitsa anthu aja kuti adziloweza pantima sabata ndi sabata ndime za m'Buku Lopatulika.
15. Mbusa ayenera kumalimbikitsa makalasi amene ali kukula.
16. Tchalitchi iyenera kukhala ndi maphunziro a m'mene tingachitire umboni kamodzi pa chaka. Izi zidzathan-diza aphunzitsi atsopano kuti aphunzire m'mene angachitire umboni ndiponso zidzalimbikitsa aphunzitsi akale aja.
17. Mbusa ayenera kumakumana ndi aphunzitsi a Sande Sukulu kamodzi pa sabata kuti aone m'mene maphunziro a Sande Sukulu ali kuyendera.
18. Tchalitchi iyenera kukhala ndi cholinga chokhala ndi makalasi a Sande Sukulu atsopano chaka chiri chonse. Zinthu izi zidzathan-diza munthu aliyense amene ali pa Sande Sukulu ndi pakuchitira umboni. Ngati tchalitchi iyamba ndi anthu 12 pa Sande Sukulu, ndipo ili ndi cholinga chomalembe munthu m'modzi pa Sande Sukulu mwezi uli wonse, tchalitchi ikhoza kukula kwambiri pa nthawi yochepa.

Ngati tchalitchi yakonzekera kuchita zimenezi, chinthu china chimene chiyenera kuchitika ndi kupeza anthu okhulu-pirika amene amabwerabwera ku Sande Sukulu. Pa ndime yachiwiriyi, tiphunzira za njira zitatu zimene zingatitha-ndize m'mene tingapezere anthu otaika.

1. Kupeza anthu otaika m'tchalitchi. Ndi chinthu chodabwitsa kwa anthu ena kuti kupeza anthu otaika m'tchalitchi. M'tchalitchi ndi pa Sande Sukulu ayenera kulemba maina a anthu onse amene amabwera ku tchalitchi ndi ku Sande Sukulu. Ngati mwatenga maina a anthu amene ali m'tchalitchi muja ndi kuonanso maina amene ali pa Sande Sukulu paja, mudzapeza zinthu ziwiri.

Choyamba, mudzapeza kuti anthu ambiri amene amabwera ku tchalitchi, saphunzira nawo Sande Sukulu. Anthu amenewa muyenera kulankhula nawo ndi kuwalimbikitsa kuti adzibwera ku Sande Sukulu sabata ndi sabata pakuti ku Sande Sukulu ndi kumene mkhristu akhoza kulimbikitsidwa. Kachiwiri, mupeza kuti anthu amene amabwera ku Sande Sukulu ena

siakhristu. Anthu amenewa amabwera kutchalitchi ndi kumapemphera. Nthawi zina mukhoza kupeza anthu amene akulira m'tchalitchi koma sanalandire Yesu Khristu kukhala monga Mpulumutsi wawo. Amenewa ndi anthu amene muyenera kulankhula nawo ndi kucheza nawo pa nthawi yapadera. Ngati zimenezi zingachitike mwa dongosolo mukhoza kuona m'mene Ambuye angakudalitsireni. Munthu amene amabwera ku Sande Sukulu akhoza kulandira Ambuye monga Mpulumutsi wake mwa msanga kuposana ndi munthu amene sabwera ku Sande Sukulu. Amakhala ndi mwayi wakumvera za njira ya Chipulumutso cha Yesu Khristu. Tchi ndi chifukwa chake tiyenera kumaphunzira nawo Sande Sukulu anthu amene sanalandire Yesu Khristu.

ANTHU AMENE TILI NAWO PAFUPI

Njira yachiwiri yopezera anthu ndi anthu amene tili nawo pafupi. Anthu amene tili nawo m'tchalitchimo akhoza kupeza anzawo mosabvuta monga abale awo. Kachiwiri, akhoza kupeza abwenzi awo. Kachitatu, akhoza kupeza anzawo amene amagwira nawo ntchito. Pakugwiritsa ntchito njira imeneyi munthu aliyense amene ali m'tchalitchi kapena pa Sande Sukulu akhoza kulemba dzina la munthu aliyense amene ali kudziwa kuti sanalandire Yesu Khristu kukhala monga Mpulumutsi wake. Mwa chitsanzo monga abale ake, abwenzi ake ndi anzake amene amagwira nawo ntchito. Anthu awa adzakhala pa m'ndandanda wakuti tsiku lina atsogoleri akawachezere ndi kuwaitana kuti abwere ku Sande Sukulu.

Mphunzitsi adzagwiritsa ntchito ichi kuti asaiwale:

Anthu amene amabwera ku Sande Sukulu ayenera kumakumbukira anthu amene ali kuwadziwa kuti sanalandire Yesu Khristu monga Mpulumutsi wawo.

1. Agogo, amuna ndi akazi.
2. Abambo ndi amayi, achemwali ndi achimwemwe.
3. Abale abambo ndi amayi ndi ana awo onse.
4. Achimwene ndi achemwali.
5. Mwamuna kapena mkazi.
6. Asuweni anu.
7. Ana anu.

8. Abwenzi a ana anu.
9. Adzukulu anu.
10. Ana achimwene anu ndi achemwali anu.
11. Anzanu amene muli nawo pafupi.
12. Anzanu amene mwagundana nawo nyumba.
13. Bwana wanu ku ntchito.
14. Anthu amene mumacheza nawo.
15. Munthu amene mumagwira naye ntchito pamodzi.

Anthu amenewa ayenera kulembedwa pa pepala imodzi maina awo ndi maadiresi awo. Tsopano maina amenewa mupereke pa Sande Sukulu iliyonse kuti mukonze nthawi yakuti mukawachezere.

KUYENDERA MADERA

Njira yachitatu ndi kupita kumene kumakhala anthuko. Anthu onse amene ali pa Sande Sukulu ayenera kugawidwa m'magulumagulu kuti ayende m'madera osiyanasiyana kukachezera anthu. Achezera munthu aliyense amene ali kukhala m'dera limenelo ndi kumafunsa zinthu izi:

1. Dzina, zaka, ndi nambala ya nyumba kapena dzina la msewu kumene nyumbayo ilili.
2. Kodi ndi chiwalo cha mpingo?
3. Ngati zili choncho, kodi dzina la mpingowo ndi chiyani?
4. Kodi alipo anthu angati m'banja lawolo?
5. Ngati munthu atakufunsani kuti, "Ngati mutafa lero, tsono Mulungu ndikukufunsani kuti, kodi chifukwa chiyani kuti ndikulole kuti ulowe Kumwambá?" Inu mukadanena kuti chiyani?
6. Kodi mukhoza kumulola kuti ayambe Sande Sukulu? Ngati zili choncho, kodi m'modzi wa pa Sande Sukulu paja siwofunika kuti abwere naye ku Sande Sukulu pa Sabata?
7. Kodi amadziwa kumene tchalitchiyo ilili?

Mukachita zimenezi mudzathandizidwa kuti mudziwe anthu amene ali m'dera lanu amene amafuna kulandira Ambuye. Zidzathandizanso mpingo kudziwa anthu amene angathe kulembedwa maina awo kuti tsiku lina mpingo ukawachezere.

Njira zonsezi zimathandiza mamembala a Sande Sukulu monga iwo ali pa udindo ofalitsa Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Izi ndi m'mene ziyenera kuchitikira, pakuti abusa sangathe kuchezero munthu aliyense, komanso mwina iwowo sangathe kuchezero bwino anthu wokha.

Pamene Sande Sukulu ili ndi udindo wochezero anthu ndi kuchitira umboni, ilinso ndi udindo wina waukulu kwambiri wochezero akhristu ofoka. Matchalitchi ambiri, anthu ambiri sabwera kutchalitchi sabata ndi sabata, anthu ena amakhala ali kudwala, ena amakhala ali ku maliro, ena ali kukalalikira mbali zina. Koma anthu ambiri amalophora kubwera kutchalitchi chifukwa cha kufoka mumzimu. Sande Sukulu ili ndi udindo wakuchitira umboni kwa anthu onse ndi kulimbikitsa anthu amene ali kufoka mumzimu kuti abwerere ku Sande Sukulu. Izi zikhoza kuchitika ngati pali chikondi chenicheni pa anthu amenewa. Mwa njira imeneyi Sande Sukulu imalimbikitsa Akhristu ofoka ndipo ndi chitsanzo cha chikondi cha Mulungu pa anthu ake.

Sande Sukulu ndi bungwe limene lingathe kuthandiza akhristu atsopano m'chikhulupiriro chawo. Nthawi zina kutchalitchi kumakhala chitsitsimutso ndipo kumapezeka anthu amene adzipereka ndi kulandira Yesu Khristu kukhala monga Mpulumutsi wawo. Koma patangopita kanthawi anthu aja saonekanso kutchalitchi kuja, mwina amangooneka anthu ochepa okha. Sande Sukulu ndi bungwe lokhalo limene lingathandize pa nkhani imeneyi. Ngati m'makalasi muja muli anthu ochepa, munthu m'modzi akhoza kusankhidwa kuti athandize akhristu atsopanowa m'chikhulupiriro chawo. Akhristu atsopanowa akhoza kuthandiza kuti Sande Sukulu ipeze anthu atsopano amene ali kufunika kuti akawachezere. Anthu amenewa ayeneranso kuphunzitsidwa kuchitira umboni ndi kubweretsa anthu kwa Yesu. Pa Sande Sukulu munthu aliyense ndi wofunika kwambiri. Nthawi ya mapemphero akhristu atsopano akhoza kuiwalidwa koma pa Sande Sukulu sangathe kuiwalidwa ndipo ngati akhala, anthu amaliba kudziwa msanga.

Palibe chimene chingathe kukulitsa tchalitchi yanu kuposana ndi Sande Sukulu. Tchalitchi yanu ifunika kukhala ndi Sande Sukulu ya mphamvu kuyambira ya ana mpaka ya akulu. Ndi njira yokhayi imene yathandiza matchalitchi athu kufikitsa Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu pa dziko lapansi pano.